KUKONGOLA KWA AL-MUSTAFA ﷺ



Shaykh-e-Tareeqat, Ameer-e-Ahl-e-Sunnat,
muyambitsi wa Dawat-e-Islami, Allamah Maulana Abu Bilal
MUHAMMAD ILYAS
ATTAR QADIRI RAZAVI

حُسن و جمالِ مصطفٰے ﷺ

Husn-o-Jamal-e-Mustafa ﷺ

KUKONGOLA KWA AL-MUSTAFA ﷺ

Kabukuka kanaperekedwa mu Chiyankhulo cha urdu ndi Majlis Al-Madina-tul-'Ilmiyyah. **Yomasulira ya (Dawat-e-Islami)** yamasulira mu chichewa. Ngati mutapeza cholakwika chilichonse pomasulira kapena mu kapangidwe, chonde dziwitsani Nthambi Yomasulira pa positi kapena imelo adilesi ili m'musiyi ndi chitsimikizo chofuna kupeza malipiro [Sawab].

Nthambi Yomasulira (Dawat-e-Islami)

Aalami Madani Markaz, Faizan-e-Madinah, Mahallah Saudagran,

Purani Sabzi Mandi, Bab-ul-Madinah, Karachi, Pakistan

UAN: ☎ +92-21-111-25-26-92 – Ext. 7213

Imelo: ✉ translation@dawateislami.net

◆

MAUMWINI ONSE NDI OTETEZEDWA

Copyright © 2026 Maktaba-tul-Madinah

Palibe gawo lililonse la kusindikiza uku lomwe litha kutulutsidwa,kapena kutumizidwa,m'mawonekedwe aliwonse kapena mwanjira iliyonse, zamagetsi, zamakina, kujambula,kujambula mu mawu kapena mwanjira ina iliyonse, popanda chilolezo cholembedwa cha Maktaba-tul-Madinah.

Kusindikizidwa koyamba: Rabi'-ul-Awwal, 1448 AH – (Sep, 2026)

Wosindikiza: Maktaba-tul-Madinah

Kuchuluka: -

ISBN: -

THANDIZO

Chonde khalani omasuka kulumikizana nafe ngati mukufuna kuthandiza pa kusindikiza kwa buku lililonse la chipembedzo kapena kabuku pofuna kutumiza thawāb kwa anthu omwe anamwalira am'banja mwanu.

Maktaba-tul-Madinah
Aalami Madani Markaz, Faizan-e-Madinah Mahallah Saudagran,
Purani Sabzi Mandi, Bab-ul-Madinah, Karachi, Pakistan

✉ **Email:** global@maktabatulmadinah.com | feedback@maktabatulmadinah.com
✆ **Phone:** +92-21-34921389-93
💻 **Web:** www.dawateislami.net | www.maktabatulmadinah.com

www.dawateislami.net

اَلْحَمْدُ لِلّٰهِ رَبِّ الْعٰلَمِيْنَ وَالصَّلٰوةُ وَالسَّلَامُ عَلٰى خَاتَمِ النَّبِيّٖنَ

اَمَّا بَعْدُ فَاَعُوْذُ بِاللّٰهِ مِنَ الشَّيْطٰنِ الرَّجِيْمِ بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْمِ

Du’a Powerenga Buku

Werengani Du’a iyi (pempho) musanawerenge buku la chipembedzo kapena musanayambe phunziro la chisilamu, mudzakumbukira china chilichonse mwaphunzira, اِنْ شَآءَاللّٰه:

اَللّٰهُمَّ افْتَحْ عَلَيْنَا حِكْمَتَكَ وَانْشُرْ
عَلَيْنَا رَحْمَتَكَ يَا ذَا الْجَلَالِ وَالْاِكْرَام

Tanthauzo

O Allah عَزَّوَجَلَّ! Titsegulireni makomo a maphunziro ndi luntha, ndipo tichitireni chisoni! E inu omwe muli wolemekezeka kwambiri komanso aulemerero! *(Al-Mustatraf, buku. 1, tsamba. 40)*

Chidziwitso:
Mufunireni zabwino Mtumiki ﷺ kamodzi musanayambe komanso kumapeto kwa Du’a.

www.dawateislami.net

M’ndandanda wa
ZOPEZEKAMO

KUKONGOLA KWA AL-MUSTAFA ﷺ	1
Du’a ya ‘Attar	1
Ubwino wa Salat ‘Alan-Nabi ﷺ	1
Kukongola kwa al-Mustafa ﷺ	3
Kukongola kwa Wokondedwa ﷺ	4
Kuwala kwa al-Mustafa ﷺ	8
Mfundo yodabwitsa yokhudza Kuwala kwa Al-Mustafa ﷺ	11
Khope ya al-Mustafa ﷺ	12
Mtima ndi chifuwa cha al-Mustafa ﷺ	16
Chifuwa chake chodala ndi mimba yake	19
Fungo labwino la Al-Mustafa ﷺ	20
Chikondi chozama cha A’la Hadrat pa Mtumiki	22
Manja ake onunkhira bwino	23
Kupambana kwa fungo lonunkhira la Mtumiki	24
Maso, makutu ndi mphuno za al-Mustafa	25
Kupambana kwa kwa makutu ake odalitsika	26
Kupambana kwa mphuno yake yodalitsika	27
Kupambana kwa maso ake odalitsika	27
Mawu ndi manja a al-Mustafa ﷺ	29
Milomo yake yodalitsika	29
Kupambana kwa lirime lake lodalitsika	30
Kupambana kwa mano ake odalitsika	31
Kulandiridwa kwa Qasidah Burdah	32
Miyendo ya al-Mustafa ﷺ	33
Msinkhu wake wodalitsika	33
Tsitsi lake lodalitsika	34
Kupambana kwa tsitsi lake lodalitsika	35
Khungu lake lodalitsika	36

www.dawateislami.net

Mapazi odalitsika a al-Mustafa ﷺ 36
Kupambana kwa mbali zakutsogolo zodalitsika za miyendo yake 37
Kupambana kwa mapazi odalitsika 38
Kupambana kwa Na’layn zodalitsika 39
Kubadwa kwa Mtumiki wokondedwa ﷺ 40
Chifundo chachikulu kwambiri 40
Madalitso pa nthawi ya kubadwa kolemekezeka 41
Onetsani chikondi pa Wokondedwayu 43
Madalitso a kukondwerera Mawlid 43
N'chifukwa chiyani kubadwa kodalitsika kudachitika Lolemba m'mwezi wa Rabi' ul Awwal? 44
Makhalidwe apadera a Mtumiki Wokondedwa ﷺ 44
Sayyiduna Jibraeel pa maso pa Mtumiki 45
Mtumiki wa dziko lonse 46
Mtumiki woyamba ﷺ 46
Kutsika kwa madalitso 47
Lirime lodalitsika la al-Mustafa ﷺ 48

www.dawateislami.net

اَلْحَمْدُ لِلّٰهِ رَبِّ الْعٰلَمِيْنَ وَالصَّلٰوةُ وَالسَّلَامُ عَلٰى خَاتَمِ النَّبِيّٖنَ

اَمَّا بَعْدُ فَاَعُوْذُ بِاللّٰهِ مِنَ الشَّيْطٰنِ الرَّجِيْمِ بِسْمِ اللّٰهِ الرَّحْمٰنِ الرَّحِيْمِ

KUKONGOLA KWA AL-MUSTAFA ﷺ

Du’a ya ‘Attar

O Mbuye wa Mustafa! Aliyense angawerenge kapena kumvetsera kabuku ka masamba 43, ‘**Kukongola kwa al-Mustafa** صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم,’ mupatseni iye kumuona Mtumiki wanu Wokongola صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم pa nthawi ya imfa yake, ndipo mukhululukireni mopanda kuwerengeredwa.

اٰمِيْن بِجَاہِ خَاتَمِ النَّبِيّٖن صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم

Ubwino wa Salat ‘Alan-Nabi ﷺ

Munthu woyera (wali) wa Allah wodziwika kwambiri, Shaykh Abdul Aziz Dabbagh رَحْمَةُ اللهِ عَلَيْه ananena kuti: Tsinde la Paradaiso ndi Kuwala kwa Mtumiki Muhammad صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم, choncho, Paradaiso imayandikira ku Kuwala kumeneko monga m’mene mwana amayandikira kwa abambo ake. Nthawi iliyonse Paradaiso ikamva kutchulidwa kwa Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم, imakhala ndi chimwemwe chochuluka ndipo imathamangira kwa iye, chifukwa kudzera mwa iye Jannah yo imakhutitsidwa. Angelo omwe ali m’mbali komanso pa mageti a Jannah amakhala otanganidwa nthawi zonse kukumbukira Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم komanso kumutumizira Salat. Chifukwa cha zimenezi, Jannah imawalakalaka ndipo imapita kwa iwo; ndipo poti angelowo ali m’mbalimbali mwa Jannah, Jannah yo imayamba kukulira m’mbali zonse zinayi. Zikanakhala kuti Allah Wamphamvu zonse sanafune, komanso anakakhala kuti sanaike malire pa Paradaiso, ikanawonekera pa nthawi ya moyo wa Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم Allah Wamphamvu zonse anaisunga paradaiso kuti

www.dawateislami.net

isawonekere, pofuna kuti chikhulupiriro chibwere kudzera m'zinthu zomwe sizioneka (Imaan bil Ghayb). *(Al-Ibreez, buku. 2, tsamba. 337)*

Wokonda Mtumiki kwambiri, A'la Hadrat, Imam-e-Ahl-e-Sunnat, Imam Ahmad Raza Khan رَحْمَةُ اللهِ عَلَيْه analemba m'njira yokongola kwambiri kuti:

Jannat hai un kay jalwah say joya-e-rang-o-bu

Ay gul hamaray gul say hai gul ko suwal-e-gul

Mafotokozedwe a ndakatulo ya A'la Hadrat: Ee Mbuye wanga صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم! Ndinu okongola modabwitsa kwambiri moti ngakhale Paradaiso imafuna kukongola komanso kafungo kabwino kuchokera kwa inu. Inu maluwa amene mukuphuka m'munda! Nanunso funani kukongola kuchokera ku duwa lowala la m'munda wa uneneri, lomwe ndi Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم.

Dekh Rizwan dasht-e-Taybah ki bahar,

Meri Jannat ka nah payega jawab

Sar se paa tak har adaa hai laajawab,

Khoobaruyon mayn nahin tera jawab

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

Kukongola kwa al-Mustafa ﷺ

(Bayan yomwe inachitika pa 1 Rabi'-ul-Awwal 1442)

Abale anga achisilamu okondedwa! Allah Wamphamvu zonse anampatsa Mtumiki wathu Wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم kukongola koti kulibe kofanana nako. Nanga kofanana nako kungapezeke bwanji? Pakuti Allah Wamphamvu zonse sanalengepo munthu wina aliyense wokongola ngati iye. Kukongola kwake kunali koti wina amanena kuti nkhope yake yodalitsika inali ngati mwezi, wina namanena kuti mizere ya kuwala imachokera pankhope yake yolemekezeka, ndipo winanso

www.dawateislami.net

amanena kuti m'dziko muno simunabwerepo munthu wina aliyense wokongola ngati iye. Ala Hadrat, Imam-e-Ahl-e-Sunnat, Imam Ahmad Raza Khan رَحْمَةُ اللهِ عَلَيْه ananena kuti:

Lam yaati nazeeruka fee nazarin, Misl-e-tau na shud paida jana,

Jag raaj ko taaj torey sar sau, Hay tujh ko shah-e-do sara jana

Mafotokozedwe a ndakatulo ya A'la Hadrat: Ee Mtumiki wa Allah صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم! Diso silinawaonepo wina aliyense wokongola ngati inu, chifukwa palibe munthu wokongola ngati inu amene anabadwapo; chipewa chachifumu cha ulamuliro pa dziko lonse chili pa mutu wanu wodalitsika, ndipo ndimakutengani inu ngati mfumu ya maiko onse awiri.

Allah Allah sheh konayn jalalat teri

farsh kiya arsh peh jary hay huqoomat teri

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

Ee inu omukonda Mtumiki! Ndakatulo za Ala Hadrat رَحْمَةُ اللهِ عَلَيْه zimagwirizana kwathunthu ndi Quran komanso Sunnah. Chifukwa chake, m'limodzi mwa mabuku odziwika bwino a Hadith pa mabuku asanu ndi limodzi akuluakulu, lotchedwa 'Tirmizi', munalembedwa kuti: Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anati, 'Athandizi anga awiri, Jibraeel ndi Mikael عَلَيْهِمَا السَّلَام ali kumwamba, ndipo athandizi anga ena awiri, Abu Bakr ndi Umar رَضِیَ اللّٰهُ عَنْهُمَا ali pa dziko lapansi.' *(Tirmizi, buku. 5, tsamba. 382, Hadith. 3700)*

Kuchokera mu Hadith imeneyi, tikuphunzira kuti Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ndi mfumu yaikulu ya ulamuliro wa kumwamba komanso dziko lapansi, chifukwa ndi mfumu yokha yomwe imakhala ndi athandizi, ndipo ufumu wake ndi waukulu bwanji, monga momwe iye صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم mwini akunenera mu Sahih Bukhari, Hadith 1344: اُعْطِيْتُ مَفَاتِيْحَ خَزَائِنِ الْاَرْض kutanthauza kuti, 'Ndinapatsidwa

www.dawateislami.net

makiyi a chuma cha dziko lapansi.' *(Bukhari, buku. 1, tsamba. 452, Hadith. 1344)* Ndiye n'chifukwa chiyani tisafuule ndi kunena mwachimwemwe kuti:

Unhay khuda nay kiya Aapnay mulk ka maliq

Unhin ke qabzay mayn Rab ke khazanay a`ay hain

Yeh kis shehenshah walay ki amad amad hay

Yeh kon shahay bala ki amad amad hay

Makki marhaba! *Madani marhaba!*

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

Kukongola kwa Wokondedwa ﷺ

Sahabi, سَيْفٌ مِّنْ سُيُوْفِ الله, yemwe ndi lupanga la malupanga a Allah, Sayyiduna Khalid Bin Waalid رضی اللّٰہ عنہ tsiku lina anafunsidwa ndi mtsogoleri wa fuko lina kuti, 'Fotokozani kukongola kwa Mtumiki wanu.' Iye رضی اللّٰہ عنہ anayankha kuti, 'Sindingathe kufotokoza mwatsatanetsatane.' Mtsogoleriyo anati, 'Ndiye fotokozani mwachidule.' Iye رضی اللّٰہ عنہ anati, 'Monga momwe Mlengi amene anamutumiza alili, Mtumiki wake nayenso ndi wangwiro moyenerera.' *(Al-Mawahib Al-Ladunya, buku. 2, tsamba. 5,mwachidule)*

سُبْحٰنَ اللّٰه! Iye anasunga nyanja yonse m'dontho limodzi! Kutanthauza kuti, ngati amene anamutumiza iye ndi Mlengi, ndipo iyeyu ndi Wokondedwa Wake, ndiye mutha kulingalira kupambana kwa kukongola kwake

Jis kay hathon kay bannae huwe hayn husn-o-jamal

Ay haseen teri ada uss ko pasand ayi hay

Baag-e-jannat mayn nirali chaman arayi hay

kiya madinay pay fida ho kay bahar ayi hay

Mlembi wa ndakatulo wotchuka wa Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم, Sahabi, Sayyiduna Hassan Bin Saabit رضی اللہ عنہ akufotokoza kukongola kwa Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم m'njira iyi yotsatirayi:

وَاَحْسَنُ مِنْكَ لَمْ تَرَقَطُّ عَيْنِيْ وَاَجْمَلُ مِنْكَ لَمْ تَلِدِ النِّسَاءُ

خُلِقْتَ مُبَرَّأً مِّنْ كُلِّ عَيْبٍ كَاَنَّكَ قَدْ خُلِقْتَ كَمَا تَشَاءُ

Kumasulira: Ee Mtumiki wa Allah صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم! Maso anga sanaonepo munthu wina aliyense wokongola kuposa inu. Ee Mtumiki wa Allah صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم! Palibe mkazi aliyense amene anabelekapo munthu wokongola ngati inu. Ee Mtumiki wa Allah صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم! Munalengedwa wopanda chofooka kapena chilema chilichonse. Ee Mtumiki wa Allah صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم! Zili ngati munalengedwa m'njira yomwe inu mwini mumafunira. *(Ruh Al-Ma'ani, gawo 11, pansi pa vesi 2, buku.11, tsamba. 83)*

Jis kay hathon ke banaye hu`ay hayn husn-o-Jamaal,

Ay haseen teri ada uss ko pasand aayi hai

Womukonda Mtumiki wina ananenanso m'njira yokongola kwambiri kuti:

Sahabah woh Sahabah jin ki har subh Eid hoti thi,

Khuda ka qurb hasil tha, Nabi ki deed hoti thi

Har Sahabi-e-Nabi	Jannati Jannati
Sab Sahabiyat bhi	Jannati Jannati
Hadrat Siddeeq bhi	Jannati Jannati
Aur Umer Farooq bhi	Jannati Jannati
Usman Ghani	Jannati Jannati
Fatima aur Ali	Jannati Jannati

www.dawateislami.net

Hayn Hassan Hussain bhi	Jannati Jannati
Hayn M'awiyah bhi	Jannati Jannati
Aur Abu Sufiyan bhi	Jannati Jannati
Walidayn Nabi	Jannati jannati

Ee inu okonda Kukongola kwa Mtumiki! Munthu wochita zabwino wa m'mbuyomu anati: Kukongola konse komanso kupambana konse kwa Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم sikunawonetsedwe kwathunthu kwa ife; pakuti zikanakhala kuti kukongola kwake konseku kunaonekera, maso athu sakanatha kumuyang'ana iye. *(Al-Mawahib Al-Ladunya, buku. 2, tsamba 5)*

Mwini kukongola komanso kupambana, Mtumiki wowala صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anati, 'Ee Abu Bakr! Palibe amene akudziwa chowonadi chenicheni cha ine kungopatula Ambuye anga.' *(Matali' Al-Musarraat, tsamba. 133)*

A'la Hadrat, Imam-e-Ahl-e-Sunnat, Imam Ahmad Raza Khan رَحْمَةُ اللهِ عَلَيْه anafotokoza bwino kwambiri za kukongola kwa Mneneri Wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم m'mawu otsatirawa:

Husn-e-Yusuf peh kattihn Msr mayn angusht-e-Zanaan,

Sar katatay hai teray naam peh mardaan-e-Arab

Ndemanga ya ndakatulo ya A'la Hadrat: Sayyiduna Yusuf عَلَيْهِ السَّلَام anabisidwa kuseri kwa nsalu yotchinga, ndipo amayi anapatsidwa mandimu kapena maapulo kuti adule, kenako Sayyiduna Yusuf عَلَيْهِ السَّلَام anaonetsedwa kwa iwo ndipo analamulidwa kuti azidula mandimuwo. Komabe, atangomuona Sayyiduna Yusuf عَلَيْهِ السَّلَام, onse anali odabwa kwambiri. Ndipo m'malo modula mandimu, anathera ndikuzidula zala zawo ndipo sanazindikire n'komwe. A'la Hadrat رَحْمَةُ اللهِ عَلَيْه anati: Amayiwo anazidula zala zawo chifukwa choona kukongola kwa Sayyiduna Yusuf عَلَيْهِ السَّلَام, koma akuluakulu a ku Arabia (Masahaba) sanadule zala zawo poona kukongola

www.dawateislami.net

kwa Mtumiki wathu صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم, m'malo mwake, iwo amavomereza kudulidwa mitu yawo chifukwa cha dzina lake lokha lodalitsika.

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

Kuwala kwa al-Mustafa ﷺ

(Bayan imene inachitika pa 3 Rabi'-ul-Awwal 1442)

Inu okonda Mtumiki! Nthawi zambiri, kukongola kwa munthu, kapena kuperewera kwake, kumaonekera pa nkhope yake. Anthu ambiri "okongola" anabadwa m'dziko lino; kukongola kwa ena kunadziwika m'mabanja mwawo, ena anatchuka m'madera mwawo, m'mizinda, m'midzi, ndi malo ena. Ndipo ngati munthu ali wokongola modabwitsa, kukongola kwake kumatamandidwa m'dziko lonse. Komabe, m'dziko lonseli, muli wina yemwe ali wokongola kwambiri komanso amene ali wooneka bwino kwambiri. Kukongola kwake sikunathere m'banja lake kapena kudera lake kokha, koma dziko lonse limavomereza kukongola kwake. Osati pa nthawi yomwe anali ndi moyo yokha, koma ngakhale patapita zaka mazana ambiri, kukongola kwake kukutamandidwabe pakati pa Aluya komanso omwe si Aluya mpaka lero lino.

Osati omutsatira okha, komanso ngakhale adani ake sangapeze cholakwika chilichonse pa khalidwe kapena maonekedwe ake mpaka lero. Ndipo kodi angachipeze bwanji, pamene Mlengi wa dziko lonse anamupatsa kukongola kwakuti aliyense amene angamuyang'ane amakhala wokonzeka kupereka moyo wake chifukwa cha iye. kukongola koyera kuyambira kumutu mpaka kumapazi kotereku ndi kwakuti ngakhale kukongola komweku kumadzinyadira chifukwa chokhala mwa iye. Iye ndiye mwini wake wa kukongola, Wokondedwa wa Allah Wamphamvu zonse, komanso Mtumiki Wotsiriza صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم. Mneneri wokondedwa wa Allah Wamphamvu zonse, Sayyiduna Yusuf عَلَيْهِ السَّلَام anali wokongola kwambiri m'chilengedwe cha Allah, koma Mneneri Wotsiriza wa Allah صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anali wokongola komanso wooneka bwino kwambiri kuposa iye, Sayyiduna Yusuf عَلَيْهِ السَّلَام anapatsidwa gawo limodzi la kukongola, pamene Mtumiki wosayerekezeka, Ngale yowala ya Sayyidatuna Aminah, صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anapatsidwa

www.dawateislami.net

kukongola kwathunthu. Dzuwa, mwezi, ndi nyenyezi zimalandira kuunika kwawo kuchokera ku kuunika kwa Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ndipo zimawala m'thambo

يَا صَاحِبَ الْجَمَالِ وَيَا سَيِّدَ الْبَشَرْ مِنْ وَّجْهِكَ الْمُنِيْرِ لَقَدْ نُوِّرَ الْقَمَرْ

لَا يُمْكِنُ الثَّنَآءُ كَمَا كَانَ حَقُّه‘ بعد از خدا بزرگ توئی قصہ مختصر

Tanthauzo: Inu mwini wake wa kukongola! Inu mbuye wa anthu onse! Inu amene mwezi umalandira kuwala kuchokera pa nkhope yanu yowala kuti uwale! Sizingatheke kukutamandani m'mene mukuyenerera; pambuyo pa Allah Wamphamvu zonse, inu ndinu wamkulu kuposa onse. Ndinu wamkulu kwambiri m'chilengedwe chonse. Ndakatulo ya mizere inayi imeneyi si ya wolemba ndakatulo wamakono, koma pali maganizo osiyanasiyana pankhaniyi: Ena amati ndakatuloyi ndi ya Shah Abdul Aziz Muhaddis Dihlvi رَحْمَةُ اللهِ عَلَيْه, ena amati ndi ya Shaykh Sa'di رَحْمَةُ اللهِ عَلَيْه, ndipo akatswiri ambiri a zachipembedzo ali ndi maganizo oti ndakatuloyi ndi ya Allamah Jami رَحْمَةُ اللهِ عَلَيْه.

Bambo a A'la Hadrat, Maulana Naqi Ali Khan رَحْمَةُ اللهِ عَلَيْه analemba pa tsamba 115 la buku la Anwar-e-Jamal-e-Mustafa kuti: Nzeru za anthu sizingathe kupirira mphamvu ya Kuwala kwa Uneneri. Iwo anapitiriza kunena kuti: Zafotokozedwa mu Hadith kuti ngati bangili la mkazi wa ku Paradaiso litaonetsedwa, likhoza kuphimba kuwala kwa dzuwa, monga m'mene dzuwa limaphimbira kuwala kwa nyenyezi. Koma maonekedwe a Mtumiki Muhammad عَلٰى صَاحِبِهَا الصَّلٰوةُ وَالسَّلَام ndi owala mosayerekezeka kuposa mkazi wa ku Paradaiso, tsono ndindani amene angathe kupirira kuwala koteroko *(Anwar-e-Jamal-e-Mustafa, tsamba. 114)*

Kiya munh hay aainah ka teri taab laa sakey

Khursheed pehlay aankh to tujh say milaa sakey

Kutanthauza kuti, kodi galasi lili ndi udindo wanji kapena mphamvu yanji kuti lithe kupirira kuwala kwa nkhope yanu? Dzuwa liyenera kukhala ndi mphamvu

www.dawateislami.net

yotha kuyang'anana nanu pamaso kaye, ndipo pambuyo pake m'pamene titha kulankhula za galasi. Maulana Hasan Raza Khan رَحْمَةُ اللهِ عَلَيْه anati:

Ik jhalak dekhnay ki taab nahin A'lam ko,

Woh agar jalwa karayn kon tamash`i ho

(Zauq-e-Na'at, tsamba. 204)

Inu okonda Mtumiki! Kukongola kwa Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم n'kophimbidwa; ngati kukongola kwake kwenikweni kunakaonetsedwa poyera, anthu a pa dziko lapansi sakanatha kupirira ngakhale kuonekera kwake kumodzi kokha. Zafotokozedwa mu Sahih Bukhari: Sayyiduna Bara Bin 'Aazib رضی اللّٰہ عنہ anati, 'Mtumiki wa Allah صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anali wokongola kwambiri kuposa anthu onse, ndipo anali ndi khalidwe labwino kwambiri kuposa anthu onse.' *(Bukhari, buku. 2, tsamba. 487, Hadith. 3549)*

Sayyidatuna Umm-e-Ma'bad رضی اللّٰہ عنہ anafotokoza kuti, 'Kutali, Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ankaoneka wokongola kwambiri, ndipo pafupi, anali wokoma komanso wooneka bwino kwambiri.' *(Dalaail Al-Nubuwwah Lil bayhaqi, buku. 1, tsamba. 279)* Sayyiduna Abu Hurayrah رضی اللّٰہ عنہ anati, "Sindinaonepo munthu aliyense wokongola kuposa Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم.' *(Shumaail Tirmizi, tsamba. 86, Hadith. 116)*

Khamah-e-Qudrat ka husn-e-dastkaari wah wah!

Kya hi tasweer apnay pyari ki sanwari wah wah!

Ndemanga ya ndakatulo ya A'la Hadrat: Kodi tinganene chiyani za ukulu ndi ulemerero wa mphamvu za Allah Wamphamvu zonse: Iye adalenga maonekedwe osayerekezeka komanso opanda ofanana nawo kwa Wokondedwa wake صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم m'njira yokongola kwambiri kuposa zonse.

www.dawateislami.net

Mfundo yodabwitsa yokhudza Kuwala kwa al-Mustafa ﷺ

Shaykh Abdul Aziz Dabbagh رَحْمَةُ اللهِ عَلَيْه ananena kuti: "M'mwezi wa Malichi, kuwala kodala kwa Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم kumagawira kupambana kwake katatu ku mbewu zonse, ndipo kudzera m'madalitso amenewa, zipatso zimamera kuchokera ku mbewuzo. Ngati kuwala kwa Mneneri Wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم kukanakhala kulibe, ndiye kuti ngakhale zipatso zimenezi sizikanakhala zilipo, nanga bwanji zinthu zina zonse? Pamene Sayyiduna Adam عَلَيْهِ السَّلَام adafika koyamba pa dziko lapansi, zipatso zikangooneka m'mitengo, zinkagwera pansi; kotero, ndi cholinga chosunga zipatsozo kuti zikhale ndi moyo, Allah Wamphamvu zonse anayikamo Kuwala kwa Muhammad صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم, Chifukwa cha zimenezi, zipatsozo zinkakhalabe m'mitengo ngakhale zitapsya kale. *(Al-Abreez, buku. 2, tsamba. 186-193)*

E inu okonda Mtumiki! Choncho, tikuzindikira kuti zipatso zotsekemera zimene timadya zili ndi Kuwala kwa Muhammad صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم. Mulinso madalitso a kuwala kwa al-Mustafa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم.

Kya noor-e-Ahmadi ka chaman mayn zuhoor hai,

Har gul mayn har shajar mayn Muhammad ka noor hai

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

Khope ya al-Mustafa ﷺ

(Bayan yomwe inachitika pa 4 Rabi'-ul-Awwal 1442)

Ee inu okonda Mawlid a Mtumiki! Chiwalo chopambana komanso cholemekezeka kwambiri m'thupi la munthu ndi nkhope yake, chifukwa pamene munthu akufuna kupereka chidwi chake kwa wina, amayang'ana kumene kuli nkhope yake. Sahabi, Sayyiduna Ka'b Bin Malik رضی اللہ عنہ anati: Mayi wina wa ku Hamdaan adandidziwitsa kuti adachita nawo Hajj limodzi ndi Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم. Ine ndidafunsa kuti, 'Kodi nkhope yodalitsidwa ya Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم' idali bwanji?' Choncho, iye adayankha kuti, 'Idali ngati

www.dawateislami.net

mwezi mu usiku umene mweziwo umakhala wathunthu pa usiku; sindidawonepo nkhope ngati yake kale lonseli kapena pambuyo pake.' *(Madarij Al-Nubuwwah, buku. 2, tsamba. 5)*

Sahabi wamkulu, Maula Ali, Mkango wa Allah رضی اللہ عنہ Nkhope yodalitsika ya Mtumiki Wokondedwa wa Allah صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم inali yozungulira pang'ono. (Kutanthauza kuti, siinali yozungulira kotheratu, ndipo chimenechi chinali chinthu chomwe ma Arabu ankachikonda kwambiri). *(Al-Mawahib Al-Ladunya, buku. 2, tsamba. 8)*

Zafotokozedwa mu 'اَلشِّفَاء بِتَعْرِفِ حُقُوْقِ الْمُصْطَفٰى' kuti: Khungu la Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم lidali loyera, maso ake odalitsidwa adali akuda, akulu komanso opatukana bwino ndipo mwa iwo munali mizere yofiira, nsidze zake za m'maso zidali zazitali, nkhope yake inkawala, nsidze zake za pamphumi zidali zopyapyala, nkhope yake yolemekezeka idali yozungulira, ndipo chipumi chake chodalitsika chinali chotakata. *(Al-shifa, tsamba. 59)*

Zatchulidwa m'nkhani ina kuti: Nkhope yodalitsika ya Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم inkawala ngati mwezi wathunthu. *(Jawahir Al-Bihar (kumasulira), buku. 3, tsamba. 252)*

Roo-e-Badr-ud-Duji dekhtay reh gaye,

Chehra-e-Wadduhaa dekhtay reh gaye

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

Ee inu okonda Mtumiki! Anthu ambiri olungama akale anayerekeza Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ndi 'Badr,' kutanthauza mwezi wathunthu, chifukwa mweziwo umatha kuoneka wathunthu. Mwezi wa pa usiku wa 14 umatchedwa 'Badr,' ndipo mwezi woyambira pa usiku woyamba mpaka wachitatu umadziwika kuti 'Hilal,' mawu oti 'Riwayaat-e-Hilal' anachokera pamenepa; ichi ndi chigawo chake chopyapyala kwambiri. Dzina linanso la Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم

www.dawateislami.net

ndi ‘Badr’. Pamene iye صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ankasamuka kuchokera ku Makkah kupita ku Madina, atsikana achichepere anamulandira ndi dzina lomwelo pamalo otchedwa ‘Saniyaat-Al-Wada’. Iwo ankaimba ndakatulo iyi:

طَلَعَ الْبَدْرُ عَلَيْنَا مِنْ ثَنِيَّاتِ الْوَدَاعِ
وَجَبَ الشُّكْرُ عَلَيْنَا مَا دَعَا لِلّٰهِ دَاعِ

Tanthauzo: (kutanthauza mwezi wathunthu) watulukira pa ife kuchokera ku mapiri a Saniyyaat-Al-Wada, ndipo n'koyenera kwa ife kuyamika nthawi zonse pamene woitanira akuitanira kwa Allah.

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

Ee inu omukonda Mtumiki! Allah Wamphamvu zonse akunena m’gawo 30, mu Surah Al-Duha:

وَالضُّحٰى ۙ﴿۱﴾ وَالَّيْلِ اِذَا سَجٰى ۙ﴿۲﴾

Ndikulumbirira nthawi ya masana. Ndi usiku pamene ukuphimba (chilichonse ndi mdima wake).

[Kanz-ul-Iman (kumasulira kwa Quran)] (Gawo 30, Surah Al-Duha, vesi 1ndi 2)

Shah Abdul Aziz Muhaddis Dihlvi رَحْمَةُ اللهِ عَلَيْه ananena mu buku 4, tsamba 411 la Tafseer Azeezi kuti: Malinga ndi ofotokoza Qur'an ena ‘ضُحیٰ’ amatanthauza kubadwa kodalitsika kwa Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم, ndipo ‘لَيْل’ amatanthauza Usiku wa Mi’raaj. Ofotokoza Qur'an enanso amati: ‘ضحیٰ’ amatanthauza nkhope yowala ya Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم, ndipo ‘لَيْل’ amatanthauza tsitsi lake lodalitsika, limene lili ngati usiku chifukwa cha kuda kwake. *(Tafseer-e-Azeezi, buku. 4, tsamba. 411)* Mufti-e-A’zam Hind رَحْمَةُ اللهِ عَلَيْه akunena izi pa bwalo la Mtumiki:

www.dawateislami.net

Dikha deejiay shaha pur noor chehrah,

Sifat mayn jis ki (وَالشَّمْس) aur (ضُحٰی) hay

Ee inu okonda Mtumiki! Kuyerekeza ndi dzuwa komanso mwezi ndi chikhalidwe cha ma Arabu, koma zenizeni zake n'zakuti palibe chilichonse choyerekezeka ndi maonekedwe komanso khalidwe la Mtumiki Wokondedwa صَلَّی اللّٰہُ عَلَیْہِ وَاٰلِہٖ وَسَلَّم. Katswiri wina wa ndakatulo ananena mokongola kwambiri kuti:

Chaand ki tarah un ko hum kahihn to mujrim hayn,

Kyun ke unki chokhat par chaand khud suwali hay

Har taraf madinay mayn bheer hay faqeeron ki

Aik denay waala hay, kul jahan suwaali hay

صَلُّوْا عَلَی الْحَبِیْب صَلَّی اللّٰہُ عَلٰی مُحَمَّد

Pamene Mtumiki Wokondedwa صَلَّی اللّٰہُ عَلَیْہِ وَاٰلِہٖ وَسَلَّم ankasangalala, nkhope yake yodalitsika inkakhala ngati galasi limene linkayamba kuonetsera makoma, zitseko komanso nkhope za anthu. *(Madarij Al-Nubuwwah, buku. 1, tsamba. 6)* Kutanthauza kuti, chilichonse chimene chinalipo pamenepo chinkaoneka pa nkhope yodalitsika ya Mtumiki Wokondedwa صَلَّی اللّٰہُ عَلَیْہِ وَاٰلِہٖ وَسَلَّم.

Utha do parda dikha do chehra kay noor-e-bari hijab mayn hayn

Zamana tareek horaha hay kay mehr kab say niqab mayn hay

Ndemanga ya ndakatulo ya A'la Hadrat: Ee Mbuye wowala صَلَّی اللّٰہُ عَلَیْہِ وَاٰلِہٖ وَسَلَّم! Chotsani chophimba pa nkhope yanu yowala ndipo tiloleni tikuoneni; kuyambira pamene nkhope yanu yodalitsika idaphimbidwa, kuli ngati mdima wafalikira paliponse. Zikanakhala kuti!

Sakrat ki jab sakhtiyan sarkar hon tary

Allah mujhay Aapnay nazaron mayn ghumana

www.dawateislami.net

Jab dam hon labon par ay shehenshah e madinah

tum jalwa dikhana mujhay kalma bhi parhana

Aaqa mera jis waqt keh dum toot raha ho

uss waqt mujhay chehra pur noor dikhana

(Wasail bakhshish, tsamba.352)

Mtima ndi chifuwa cha al-Mustafa ﷺ

(Bayan imene inachitika pa 5 Rabi'-ul-Awwal 1442)

Ee inu omukonda Mtumiki! Mtumiki Womaliza wa Allah Wamphamvu zonse, Sayyiduna Muhammad صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم siku lina ananena pamaso pa Allah Wamphamvu zonse kuti: 'Inu Allah Wamphamvu zonse! Munamupanga Sayyiduna Ibrahim عَلَيْهِ السَّلَام kukhala Khalil wanu (kutanthauza bwenzi lanu), You granted Sayyiduna Musa عَلَيْهِ السَّلَام ulemerero wa kalam (wolankhula) nanu, munapanga mapiri ndi chitsulo kukhala pansi pa ulamuliro wa Sayyiduna Dawood عَلَيْهِ السَّلَام, dipo ma Jinn, anthu komanso nyama zonse kukhala pansi pa ulamuliro wa Sayyiduna Sulayman عَلَيْهِ السَّلَام; kodi ndi ulemerero ndi ubwino wanji wapadera umene mwandipatsa ine? Pa chifukwa chimenechi, Surah Alam-Nashrah idatsitsidwa, momwe munanenedwa kuti:

اَلَمْ نَشْرَحْ لَكَ صَدْرَكَ ۙ﴿۱﴾ وَ وَضَعْنَا عَنْكَ وِزْرَكَ ۙ﴿۲﴾ الَّذِیْۤ اَنْقَضَ ظَهْرَكَ ۙ﴿۳﴾ وَ رَفَعْنَا لَكَ ذِكْرَكَ ؕ﴿۴﴾

Kodi Sitidatsegule chifuwa chako (Ee Wokondedwa)? Ndipo (Ife) tidakuchotsera mtolo umenewo (Ee Wokondedwa), umene udathyola msana wako (mawu osonyeza nkhawa yaikulu). Ndipo takukweza kutchulidwa kwako chifukwa cha iwe,

[Kanz-ul-Iman (kumasulira kwa Quran)] (Gawo 30, Surah Alam Nashrah, mavesi 1 ndi 4)

www.dawateislami.net

Zili ngati kuti zinanenedwa kuti: Ee Wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم! Ngati ife tidamutenga Sayyiduna Ibrahim عَلَيْهِ السَّلَام kukhala Khalil Wathu (bwenzi Lathu), ndiye Ife tidakutsegulira chifuwa chako ndi kuwala kwa chidziwitso, nzeru komanso kuzindikira kwauzimu (kutanthauza kundizindikira Ine); ngati Ife tidamupatsa Sayyiduna Musa عَلَيْهِ السَّلَام ulemerero wolankhula nafe, ndiye ife tidakuitana ku Laa-Makan (kubwalo Lathu mu Usiku wa Mi'raaj) ndipo tidakupatsa mwayi wotiona; ngati Ife tidapatsa Sayyiduna Dawood komanso Sayyiduna Sulayman عَلَيْهِمَا السَّلَام ulamuliro pa zinthu zochepa za m'dziko lino, ndiye ife tidakupatsa ufumu wa kumwamba, kotero kuti angelo a kumeneko amakhala m'bwalo mwako ngati atumiki.

(Al Kalam al-awdah fi Tafseer alam Nashrah, tsamba. 14, mwachidule)

Rafay zikar-e-jalalat pay Arfa'a-e-Durood

Sharh-e-Sadar-e-Sadarat pay lakhon salam

Dil samjh se wara hay magar yun kahoon

Gunchah raaz-e-wehdat peh lakhon salam

Ndemanga ya ndakatulo ya A'la Hadrat: Ee Mtumiki wa Allah صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم! a kukwezedwa kwa ulemerero wanu komanso ukulu wanu umene Allah Wamphamvu zonse wautchula m'Qur'an, pakhale madalitso (Salat) osawerengeka; pa chozizwitsa chachikulu cha kutsegulidwa kwa chifuwa chanu, pakhale mtendere (Salam) wochuluka kwambiri. Ee Mtumiki wa Allah صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم! Kupambana kwa chifuwa chanu cholemekezeka ndi kopitirira malire a nzeru zanga, ndipo ndingathe kunena izi zokha: chifuwa chodalitsika ichi ndi nkhokwe ya zinsinsi za Allah; Salam yosawerengeka ikhale pa icho.

Zikanakhala kuti m'masiku odalitsika a Mawlid awa, zokhumba zolemekezeka za Mufti-e-A'zam Hind Maulana Mustafa Raza Khan Ibn Imam Ahmad Raza Khan رَحِمَهُمَا اللّٰه zilandiridwe m'malo mwathu.

www.dawateislami.net

Rouf aisay hayn aur yeh raheem hayn itnay

keh girtay parton ko seenay laganay aye hayn

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

Ee inu omukonda Kubadwa kwa Mtumiki! Pamene ayyiduna Jibreel عَلَيْهِ السَّلَام adatsuka mtima woyera wa Mtumiki ndi madzi a Zam Zam pambuyo potsegula chifuwa chake chodalitsika, iye adanena kuti, 'Uli ndi maso awiri amene amaona, komanso makutu awiri amene amamva.'

(Fath Al-Bari, buku. 14, tsamba. 407, Hadith. 7517)

Ghazali wa m'nthawi yake, Allamah Sayyid Ahmad Sa'eed Kazmi رَحْمَةُ اللهِ عَلَيْه anati: Makutu komanso maso amenewa a mtima wake wodalitsika ndi oonera komanso omvera zinthu zoonadi zomwe zili kutali kwambiri kuposa zomwe zimadziwika m'dziko lino mwa mthawi zonse. Monga momwe Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم mwiniwake ananenera kuti, 'Ine ndimaona zimene inu simungathe kuziona, ndipo ndimamva zimene inu simungathe kuzimva.' *(Maqalat-e-Kaazimi, buku. 1, tsamba. 160, amended)*

Door-o-nazdeeq ke sun'nay walay wo kaan

Kaan-e-laal-e-karamat peh lakhon salam

Jis taraf uth gayi dam mayn dam agaya

uss nigah-e-anayat peh lakhon salam

(Hadaiq-e-Bakhshish, tsamba. 300)

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

Chifuwa chake chodala ndi mimba yake

Hujja-tul-Islam, Imam Abu Haamid Muhammad Bin Muhammad Bin

Muhammad Ghazali رَحْمَةُ اللهِ عَلَيْه nalemba kuti: Chifuwa chodalitsika cha Mtumiki wathu Wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم chinali chotakata. Palibe mbali ina ya mnofu yomwe inali yotuluka kuposa inzake, koma mbali zonse zinali za mlingo umodzi ngati galasi, ndipo chinali choyera ngati mwezi. Panali kamzere kopyapyala ka tsitsi kochokera kumtunda kwa chifuwa chake chodalitsika mpaka kumchombo wake wodalitsika, ndipo panalibenso tsitsi lina pachifuwa chake cholemekezeka kapena pa mimba pake. *(Ihya al-Uloom, buku. 2, tsamba. 470)*

Allamah Yusuf Bin Ismail Nabhani رَحْمَةُ اللهِ عَلَيْه anati: Zafotokozedwa mu nkhani ina kuti mimba yake yodalitsika inali yolingana ndi chifuwa chake chodalitsika; mimba sinali yotuluka kuposa chifuwa, ndipo chifuwa sichinali chotuluka kuposa mimba. Sayyidatuna Umm Haani رَضِیَ اللّٰہُ عَنْہَا ananena kuti: 'Ndidawona mimba yodalitsika ya Mtumiki wa Allah صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ndipo inali ngati mapepala amene aikidwa pamwamba pa anzake komanso opindidwa. *(Jawahir al-bihar (kumasulira), buku. 3, tsamba. 263)*

Kul jahan mulk aur jau ki roti ghiza

Uss shikam ki qanaa'at peh lakhon salaam

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

Fungo labwino la al-Mustafa ﷺ

(Bayan imene inachitika pa 6 Rabi'-ul-Awwal 1442)

Jaa ke sabaa tu ko`o-e-Muhammad

Laa kay soonghaa Khushboo-e-Muhammad

Ee inu omukonda Mtumiki! Monga momwe Mtumiki Wokondedwa komanso Womaliza wa Allah صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم analibe wofanana naye pa kukongola kwake, chimodzimodzinso fungo lake linalibe lofanana nalo. Fungo labwino kwambiri loterolo linkatuluka m'thupi lake loyera kotero kuti munthu aliyense amene

www.dawateislami.net

amalidziwa bwino amadziwa kuti Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم wadutsa pamalo amenewa.

Anbar zameen 'abeer huwa mushk tar gubar!

Adna si yeh shakht teri rah guzar ki hay

Ndemanga ya ndakatulo ya A'la Hadrat: Paliponse pamene Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ankayenda, chizindikiro chakuti iye صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anadutsa pamalo pamenepo chidali chakuti nthaka komanso mlengalenga zinkadzaza ndi fungo labwino kuposa maski, amba komanso Abeer.

Abale achisilamu okondedwa! Amba (Ambergris) ndi mafuta onunkhira okwera mtengo kwambiri omwe amapezeka ku nsomba zamtundu wapadera. 'Abeer ndi ufa onunkhira omwe umapangidwa posakaniza mafuta onunkhira osiyanasiyana, mtengo wa sandalwood, ndi zina zotero, ndipo amawazidwa pa zovala, monga momwe amachitira ndi mafuta onunkhira opopera pa thupi omwe amapezeka masiku ano. Maski ndi mafuta onunkhira amtengo wapatali kwambiri omwe amatengedwa kuchokera pamchombo wa mbawala, ndipo amapezeka mwa mbawala zamtundu winawake zokha.

Ee inu okonda ma Sahabah komanso Ahl-al-Bayt! Werengani mawu a ma Sahabah odala رَضِیَ اللّٰہُ عَنْہُم omwe anamva fungo labwino lotuluka m'thupi lodalitsika la Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم, ndipo sangalalani. Sayyiduna Jabir Bin Abdullah رضی اللہ عنہ ananena kuti: Nthawi iliyonse yomwe Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ankadutsa mu msewu kapena pa msika, ndipo munthu wina akadzadutsa pamalopo pambuyo pake, ankazindikira kudzera m'fungo labwino la mumpweya kuti Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم wadutsa pamenepo. *(Daarimi, buku. 1, tsamba. 45, Hadith. 66; Al-Shifa, buku. 1, tsamba. 63)*

Guzray jis rah say wo sayyed wala ho kar

Reh gayi sari zameen ambar-e-sara ho kar

Ndemanga ya ndakatulo ya A'la Hadrat: Paliponse pamene Mtumiki wathu wolemekezeka komanso wapamwamba kwambiri صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ankadutsa, nthaka

www.dawateislami.net

yonseyo inkasanduka Ambar-e-Saara, kutanthauza kuti inkakhala ndi fungo labwino komanso lopambana kwambiri. Fungo la amba (Ambar) lilibe lofana nalo, koma Ambar-e-Saara ndi lopambana kwambiri kuposa pamenepo.

Chikondi chozama cha A'la Hadrat pa Mtumiki

Allah Allah! Lilime la A'la Hadrat رَحْمَةُ اللهِ عَلَيْه ndi lilime la chikondi, ndipo cholembera chake ndi cholembera cha chikondi, ndipo kumeneku ndiye kusiyana kwake. Ndakatulo yomwe A'la Hadrat رَحْمَةُ اللهِ عَلَيْه analemba inali Kalam-ul-Imam komanso Imam-ul-Kalam, kutanthauza kuti ndakatulo ya Imam, komanso Imam wa ndakatulo. Kodi A'la Hadrat رَحْمَةُ اللهِ عَلَيْه amapempha chiyani kuti athe kulemba matamando a Mtumiki?

Tubaa mayn jo sab say unchi nazukh seedih nikli shaakh

Mangoon na'at Nabi likhnay ko Roh-e-Qudus say aisi shaakh

Ndemanga ya ndakatulo ya A'la Hadrat: سُبْحٰنَ اللّٰه! Toobaa ndi mtengo wa ku Paradaiso womwe ndi wautali kwambiri, ndipo nthambi zake ndi zochuluka kwambiri kotero kuti zimafika nyumba ya munthu aliyense wokhala m'Paradaiso. A'la Hadrat رَحْمَةُ اللهِ عَلَيْه anati: Ndidzamupempha Sayyiduna Jibreel عَلَيْهِ السَّلَام kuti andipatse nthambi yayitali kwambiri, yofewa komanso yowongoka kwambiri kuchokera pamtengo wautali kwambiri wa ku Paradaiso, Tooba, kuti ndithe kulembera matamando a Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم pogwiritsa ntchito nthambiyo. Kale lonse, anthu ankalemba poviika cholembera chamtengo mu inki; choncho, cholembera chomwe A'la Hadrat رَحْمَةُ اللهِ عَلَيْه anaonetsa khumbo lofuna kukhala nacho ndi cholembera chomwe diso lina lililonse silinachionepo komanso khutu lina lililonse silinachimvepo.

Tingathe kumva chabe za madalitso aku Paradaiso; koma sitingathe kuwamvetsa. Madalitso aku Paradaiso ndi oti nzeru sizingathe n'komwe kuwayerekezera kapena kuwaganizira. Padakali pano tikumva za madalitso aku Paradaiso ndipo tikukhutiritsa mitima yathu, koma اِنْ شَآءَاللّٰه, tikadzalowa m'Paradaiso kudzera m'kuolowa manja kwa Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم, pamenepo m'pamene tidzadziwe kuti madalitso a m'Paradaiso ndi otani kwenikweni.

www.dawateislami.net

Bagh-e-jannat mayn Muhammad muskuratay howay jaingay

phool rehmat kay jharaingay hum uthatay jaingay

Manja ake onunkhira

Zafotokozedwa mu Sahih Muslim kuti kapolo wa Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم, Sayyiduna Anas رضی اللہ عنہ, anati: 'Sandinamvepo kununhira kwa amba aliyense, maski aliyense wa mbawala, kapena chinthu china chilichonse chonunkhira kwambiri kuposa fungo lonunkhira la thupi lodalitsika la Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم.' *(Muslim, tsamba. 978, Hadith. 6053)* Sayyiduna Jabir Bin Samurah رضی اللہ عنہ anafotokoza kuti: Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anadutsitsa dzanja lake pamasaya anga (monga momwe timapukutira dzanja lathu pankhope za ana), ndipo ndinamva kuzizira kwinakwake komanso fungo labwino kuchokera m'manja ake odalitsika ngati kuti iye صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم adali atangotulutsa kumene dzanja lake mubokosi la wogulitsa mafuta onunkhira. *(Muslim, tsamba. 978, Hadith. 6052)*

Wah aay itar-e-khuda saz mehekana tera

khobro miltay hayn kapron mayn paseenah tera

(Zooq-e-Na'at, safhah. 23)

Ndemanga ya ndakatulo ya Maulana Hasan: Ee fungo lonunkhira lopangidwa ndi Allah Wamphamvu zonse! Ndi kwakukulu bwanji kupambana kwako komanso fungo lako, loti ngati anthu okongola akadakhala kuti apatsidwa thukuta lako, akadakhala akulipaka pa zovala zawo. Komanso, zatsimikiziridwa kuti ma Sahabah رضی اللہ عنہم ankatenga thukuta lodalitsika la Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم n'kumalipaka pa zovala zawo.

Kupambana kwa fungo lonunkhira la Mtumiki

Pamene Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم wasisita dzanja lake lodalitsika pamutu pa mwana, zinkadziwika kudzera mu fungo labwino kuti Mtumiki

www.dawateislami.net

Wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم wasisita dzanja lake lodalitsika pa mwanayo. Pamene Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم wagwirana chanza ndi munthu wina, munthuyo amakhalabe wonunkhira bwino tsiku lonselo. *(Seerat-e-Mustafa, tsamba. 578, Seerat-e-Rasool-e-Arabi, tsamba. 263)*

Ee inu omukonda Mtumiki! Iye amene malovu ake odalitsika ali ndi machiritso, iye amene thupi lake lonse ndi lafungo labwino, kwenikweni, iye amene thukuta lake limagwiritsidwa ntchito ngati mafuta onunkhira, ndipo munthu amene wazipaka amakhala wonunkhira bwino kwambiri kuposa anthu onse; kodi ndani amene angathe kutchula makhalidwe a munthu odalitsika ameneyu! Woyera wamkulu wa njira ya Qadiriyyah Razawiyyah, Sayyiduna Abu Bakr Shibli رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه anati: Nthaka ya ku Madina Munawwarah ili ndi fungo labwino lapadera limene lili lonunkhira bwino kuposa maski. *(Madarij al-Nubuwwah, buku. 1, tsamba. 24)*

Ittar jannat mayn bhi aisi khushboo nhi

jaysi khushboo Nabi kay paseenay mayn hay

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

Maso, makutu ndi mphuno za al-Mustafa

(Bayan imene inachitika pa 7 Rabi'-ul-Awwal 1442)

Abale anga achisilamu okondedwa! Mphamvu zisanu zozindikira zinthu nazonso ndi zina mwa madalitso a Allah Wamphamvu zonse; mphamvu zisanuzi ndi mphamvu yoona, yokumva, yolawa, yonunkhiza, komanso yokhudza. Kuti munthu akhale ndi mphamvu zokwanira m'maso mwake, m'makutu, pa lilime, m'mphuno, komanso m'manja mwake ndi mphatso yaikulu yochokera kwa Allah Wamphamvu zonse. Chizolowezi komanso khalidwe lililonse la Mtumiki wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم limene timaliyang'ana, kudzera mu chisomo chapadera cha Allah Wamphamvu zonse, limapezeka pa mlingo wapamwamba kwambiri mwa iye. Chowonadi ndi chakuti, tsitsi lililonse la Wokondedwa wa Allah Wamphamvu zonse wopanda wofana naye صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ndi labwino.

www.dawateislami.net

Al garz un kay har mun pay bayhad durood

Unn kay har kho-o-khaslat pay lakhon salam

Mafotokozedwe a ndakatulo ya A'la Hadrat: Mawu akuti 'Mu' akutanthauza tsitsi. Pamene ankafotokoza mbali zosiyanasiyana za ulemerero wa Mtumiki wokondedwa, A'la Hadrat رَحْمَةُ اللهِ عَلَيْه Mwachidule, zifundo zosawerengeka komanso Salat zikhale pa tsitsi lililonse la Mtumiki wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم, ndipo Salam yochuluka ikhale pa khalidwe lililonse lodala la iye!

Kupambana kwa makutu ake odalitsika

Ee inu omukonda Mtumiki! Makutu odala a Mtumiki wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anali angwiro kwambiri, ndipo kupambana kwa makutu odalawa kunali koti palibe amene adalandirapo ofanana nawo ndipo palibenso amene adzalandire. Iwo amamva kulira kwa mitambo kuchokera pa mtunda wa mailosi masauzande ambiri. Zafotokozedwa mu Tirmizi kuti: Mtumiki wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم said, 'anati, 'Ndithudi, ine ndimaona zimene inu simuona, ndipo ndimamva zimene inu simumva.' *(Tirmizi, buku. 4, tsamba. 141, Hadith. 2319)*

Ae karam ki kaan ay gosh-e-Huzoor

Sun le faryaad-e-ghareebaan Al-ghiyaas

Mafotokozedwe a ndakatulo ya Maulana Hasan: Ee Mtumiki wa Allah صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم! Inu muli ndi kuwolowa manja komanso chisomo chachikulu kwambiri, makutu anu odala amve madandaulo owawa a anthu osauka ngati ife.

Kupambana kwa mphuno yake yodalitsika

Abale anga achisilamu okondedwa! Mbuye wanga صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anali wopanda cholakwika chilichonse m'mbali iliyonse, chiwalo chilichonse cha thupi lake chinali cholingana bwino kwambiri, moti palibe amene akanatha kumuloza chala. Mphuno yodalitsika ya Mtumiki wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم nali yayitali, yowonda komanso yokwera pang'ono pakati, yomwe nthawi zonse inali kutulutsa kuwala,

www.dawateislami.net

ndipo inali yoyenera komanso yokongola m'mbali iliyonse. *(Al Mawahib al-Ladunya, buku. 2, tsamba. 16)*

Mayang'anidwe a Mtumiki wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم nthawi zambiri amakhala moyang'ana pansi chifukwa cha kudzichepetsa komanso manyazi aulemu, koma pamene iye صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم amkakweza maso ake, amatha kuona Arsh Yapamwamba komanso Lawh Mahfooz (Gome Lotetezedwa).

Kupambana kwa maso ake odalitsika

Abale anga achisilamu okondedwa! Maso odalitsika a Mtumiki wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anali okongola kwambiri moti aliyense amene angawayang'ane akhoza kudzipereka nsembe yekha chifukwa cha iwo. Zafotokozedwa mu Tirmizi kuchokera kwa Sayyiduna Maula Ali رضی اللہ عنہ kuti maso a Mtumiki wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ankaoneka ngati ali ndi Kohl (kutanthauza kuti, ngakhale popanda kupaka Kohl, ankaoneka ngati ali ndi kohl kale), ndipo nsidze zake zolemekezeka zinali zambiri komanso zazitali. *(Shumaail Tirmizi, tsamba. 19, Hadith 6)*

Sayyiduna Hind Bin Abi Haalah رضی اللہ عنہ ananena kuti, 'Nsidze zodalitsika za Mtumiki wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم zinali zazikulu m'kukula kwake ndipo kuchuluka kwa tsitsi la pamenepo linali loyenera; osati lochuluka kwambiri kapena lochepa kwambiri, ndipo kuchokera patali, zinkaoneka zolumikizana.' *(Al-wafa Li-Ibn Juzi, buku. 2, tsamba. 7)*

Kodi tinganene chiyani za mphamvu za maso odalitsika amenewa! Sayyiduna Abdullah Bin Abbas رضی اللہ عنہ ananena kuti, 'Mtumiki wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ankatha kuona usiku mofanana ndendende ndi m'mene ankatha kuonera mu kuwala kwa mam'mawa.' *(Dalaail al-Nubuwwah, buku. 6, tsamba. 75)*

Hoon kar do tau gardoon ki bina gir jaaye

Abru jo khichey taygh-e-qazaa kir jaaye

www.dawateislami.net

Aay Sahib-e-Qawsayn bas ab radd nah karay

Sehmey huwon se teer-e-balaa phir jaaye

Mafotokozedwe a ndakatulo ya A'la Hadrat: Ee Mtumiki wa Allah صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم! Kodi tinganene chiyani za kukongola kwanu komanso ulemerero wanu, woti munakakhala mwanena kuti 'Hoon' maziko a thambo angagwedezeke, ndipo ngati nsidze zanu zodalitsika zitangosuntha pang'ono, zolembedwa za m'tsogolo (chikhonzero) zingasinthe. Ee inu amene munaonana ndi Allah Wamphamvu zonse pa Usiku wa Mi'raaj! Chonde tisonyezeni chisomo kuti masoka, mavuto, komanso masautso atichokere ife anthu amantha komanso ofooka

Girdaab e balaa mein phans ke koi tayba ki taraf jab takta hai

Sultan e Madina khud aa kar bigri ko banaya kartey hein

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

Mawu ndi manja a al-Mustafa ﷺ

(Bayan imene inachitika pa 8 Rabi'-ul-Awwal 1442)

Abale anga achisilamu okondedwa! N'kutheka kuti munaonapo maluwa a rozi akutumbuka m'minda. Tsopano mundilole ndikuuzeni za rozi lokongola limene silingopangitsa munda umodzi wokha kuoneka, koma m'malo mwake, minda yambiri imachokera mwa ilo. Limenelo ndi milomo yofewa, yokopa, komanso yaulemerero ya Mtumiki wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم yomwe ndi yofewa kwambiri kuposa masamba a maluwa a rozi atsopano.

Woh gul hai labhaa e naazuk un ke, hazaaron jhartey hein phool jin say

Gulab Gulshan mein dekhey bulbul, yeh dekh Gulshan gulab mayn hay

Mafotokozedwe a ndakatulo ya A'la Hadrat: Ee Mtumiki wa Allah صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم! Milomo yanu yokongola kwambiri ngati maluwa a rozi ndi yofewa komanso yosalala kwambiri moti si duwa limodzi lokha, kapena maluwa zana limodzi amene

www.dawateislami.net

amachokera mwa iwo, koma m'malo mwake, maluwa masauzande ambiri amachokera mwa iwo. Ee mbalame ya nightingale, iwe wokonda maluwa! Munaona mitundu yonse ya maluwa a rozi m'minda yosawerengeka, koma yang'anani pa milomo yodalitsika ya Wokondedwa wanga صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم; iyoyo ndi duwa la rozi lomwe lili ndi minda yambiri mwa ilo.

Milomo yake yodalitsika

Ee inu omukonda Mtumiki! Milomo yodalitsika ya Mtumiki wowala ndi yokongola kwambiri kuposa milomo ya zolengedwa zonse. *(Mawahib al-Ladunya, buku. 2, tsamba. 17)* Pamene iye (Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم) anatsitsidwa m'manda mwake olemekezeka, milomo yake yodalitsika inkayenda, choncho ena mwa Masahaba anayandikitsa makutu awo ndipo anamumva akunena motsitsa mawu kuti, 'Ummati, Ummati.' *(Fatawa Razawiyyah, buku. 30, tsamba. 717,zosinthidwa)*

Jinhayn marqad mayn taa hashr Ummati keh kar pukaaro gay

Humein bhi yaad kar lo un mayn sadaqah apni rahmat ka

Mafotokozedwe a ndakatulo ya A'la Hadrat: Ee Mtumiki wa Allah صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم! Chifukwa cha chifundo chanu, anthu odala amene munawatchula kuti 'Ummati' m'manda mwanu, ndiponso amene mukutanthauza, tiphatikizeninso ife pakati pa okhulupirira amenewo. Ndakatulo ya A'la Hadrat رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه ndi yozama kwambiri, ndipo zili ngati ndime ziwirizi zili ndi Du'a yoteteza chikhulupiriro. Mosakayikira, 'Ummah' akutanthauza anthu amene analandira kuitana kwake kopita ku Chisilamu ndipo anachoka m'dziko lino ali ndi chikhulupiriro chokhazikika.

Kupambana kwa lilime lake lodalitsika

Lilime lake lodalitsika linali lokongola kwambiri ndithu, ndipo panalibe wina aliyense amene anali ndi mawu omveka bwino kapena amene ankayankhula mokoma kuposa iye. *(Jawahir Al bihar (zomasuliridwa) buku. 3, tsamba. 260)*

Sartaaba qadam hay tan-e-sultan-e-zaman phool

Lab phool, dahan phool, zaqan phool, badan phool

www.dawateislami.net

Mafotokozedwe a ndakatulo ya A'la Hadrat: Thupi lodalitsika la mbuye wanga, mfumu ya dziko lonse صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ndi lofewa ngati duwa kuyambira kumutu mpaka kumapazi; milomo yake yodalitsika ndi duwa, pakamwa pake podalitsika ndi duwa, chibwano chake chodalitsika ndi duwa, ndipo thupi lake lonse ndi duwanso.

Kupambana kwa mano ake odalitsika

Ee inu omukonda Mtumiki! Pakamwa pake podalitsika panali pokulirapo pang'ono ndipo mano ake odalitsika anali osalumikizana mwathunthu, m'malo mwake, anali ndi mipata pang'ono pakati pake. Sayyiduna Abdullah Bin Abbas رَضِیَ اللّٰہُ عَنْہُمَا anati, 'Pamene Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ankayankhula, kuwala kunkatuluka m'mano mwake akutsogolo.' Sayyiduna Abu Hurayrah رضی اللہ عنہ ananena kuti, 'Kakhazikitsidwe ka mano odalitsika a Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم m'nkhama komanso m'nsagwada mwake kanali kokongola kwambiri, ndipo mndandanda wawo unali wokongola kwathunthu.' Imam Buseeri رَحْمَةُ اللهِ عَلَيْه akunena izi mu ndakatulo yake ya Chiarabu yodziwika bwino ya 'Qasidah Burdah:

كَاَنَّهَا اللُّؤْلُؤُ الْمَكْنُوْنُ فِيْ صَدَفٍ مِنْ مَّعْدِنَيْ مَنْطِقٍ مِّنْهُ وَمُبْتَسَمِ

Tanthauzo: Zili ngati kuti ngale zobisika mkhanu zam'madzi (oysters) zachokera m'migodi iwiri ya kalankhulidwe kake kolemekezeka komanso kumwetulira kwake(lilime ndi milomo yake yodalitsika). Tanthauzo la zimenezi ndi lakuti: Mayankhulidwe odalitsika komanso mano odalitsika a Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم okongola kwambiri komanso onyezimira kuposa ngale zowala. *(Kashf-e-Burdah, tsamba. 231)*

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

Kulandiridwa kwa Qasidah Burdah

Imam Jalaluddin Mohali Shaafi'i رَحْمَةُ اللهِ عَلَيْه ananena kuti: Ena mwa anthu oyera am'mbuyomu ananena kuti anamuwona Sayyiduna Abu Bakr Siddeeq رضی اللہ عنہ ku

www.dawateislami.net

maloto kumene iye رضی اللہ عنہ ankamawerenga mzere wa ndakatuloyi komanso mzere wa m'mbuyo mwake m'njira yokongola poyamikira Mtumiki Wokondedwa صَلَّی اللّٰہُ عَلَیْہِ وَاٰلِہٖ وَسَلَّم. *(Sharh Al-Qaari Alal Burdah, tsamba. 300)*

Ee inu omukonda Mtumiki! Pamene Mtumiki wathu Wokondedwa صَلَّی اللّٰہُ عَلَیْہِ وَاٰلِہٖ وَسَلَّم ankati akamapereka Khutbah, aliyense ankatha kumva mawu ake odalitsika. Pa nthawi ina, iye صَلَّی اللّٰہُ عَلَیْہِ وَاٰلِہٖ وَسَلَّم ananena izi mu Khutbah: 'اِجْلِسُوْا', kutanthauza kuti, 'Khalani pansi.' Choncho, Sahabi, Sayyiduna Abdullah Bin Rawahah رضی اللہ عنہ anamva mawu ake odalitsika kuchokera kudera (lakutali) la Bani Tamim ndipo anakhala pansi nthawi yomweyo. *(Jawahir al-bihaar (zomasuliridwa) buku. 3, tsamba. 261)* Amenewa anali Masahaba omvera. Choncho, n'chifukwa chiyani ife tisanene kuti:

Har Sahabi-e-Nabi	Jannati Jannati
Sab Sahabiyat bhi	Jannati Jannati
Hadrat Siddeeq bhi	Jannati Jannati
Aur Umer Farooq bhi	Jannati Jannati
Usman Ghani	Jannati Jannati
Fatima aur Ali	Jannati Jannati
Hayn Hassan Hussain bhi	Jannati Jannati
Hayn M'awiyah bhi	Jannati Jannati
Aur Abu Sufiyan bhi	Jannati Jannati
Walidayn Nabi	Jannati jannati

Mapewa odalitsika a Mtumiki Wokondedwa صَلَّی اللّٰہُ عَلَیْہِ وَاٰلِہٖ وَسَلَّم anali otakata (otakasuka) ndipo anali odzaza ndi mnofu. *(Al- wafa Li Ibn Jazi, buku. 2, tsamba. 12)* Manja ake odalitsika anali ofewa kuposa silika, ozizira kuposa ayezi, ndiponso amphamvu

www.dawateislami.net

kwambiri, ndipo zikhatho zake zofewa zinali zodzaza ndi mnofu. *(Madarij al-Nubuwwah, buku. 1, tsamba. 25)*

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

Miyendo ya al-Mustafa ﷺ

(Bayan imene inachitika pa 9 Rabi'-ul-Awwal 1442)

Msinkhu wake wodalitsika

Ee inu okonda Mawlid a Mtumiki! Msinkhu wa Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم sunali wautali kwambiri kapena waufupi kwambiri, m'malo mwake, pamene iye صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ankayenda yekha, iye صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ankaoneka wamsinkhu wapakatikati. Kutanthauza kuti, pamene iye صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ankayenda, zimanenedwa kuti anali wa msinkhu wapakati. Komabe, pamene munthu wamtali ankayenda pambali pake, chinali chozizwitsa cha Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم kuti iye ankaoneka wamtali kuposa munthuyo. Nthawi zina, pamene anthu awiri ataliatali anali pambali pake, iye صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ankaoneka wamtali mozizwitsa kuposa onse awiriwo. When they would both move away from him, they would be referred to as being tall, and the Beloved ProphePamene onse awiriwo achokapo pambali pake, iwo ankategedwa ngati ataliatali, ndipo Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ankaoneka kukhala wa msinkhu wapakati.

Ala Hadrat, Imam-e-Ahl-e-Sunnat, Imam Ahmad Raza Khan رَحْمَةُ اللهِ عَلَيْه anati:

Tera qadd-e-Mubarak Gulshan-e-rehmat ki daali hai

Issey bau kar tere Rabb ne binaa rehmat ki daali hai

Mafotokozedwe a ndakatulo ya A'la Hadrat: Ee Mtumiki wa Allah صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم! Msinkhu wanu ndi nthambi ya 'duwa lofiira la chifundo,' pakuti Allah Wamphamvu zonse anakulengani ndipo anakupangani kukhala maziko a chifundo ku chilengedwe chonse.

www.dawateislami.net

Tsitsi lake lodalitsika

Okondedwa abale a Chisilamu! Tsitsi lodalitsika la Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم linali lokongola kwambiri. Silinali lowongoka kwambiri ndipo silinali lopiringizika kwambiri. Pamene iye صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ankalipesa, linkaoneka ngati mafunde a mchenga. Zimanenedwa mu nkhani (Hadith) kuti: Tsitsi lodalitsika la Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم nthawi zina linkafika pakati pa khutu lake, nthawi zina mpaka ku nsonga za makutu ake, ndipo nthawi zina likatalika, linkakhudza mapewa ake odalitsika. *(Shumaail Tirmizi, tsamba. 81, 34-35, Hadith. 4, 23 - 26)* Nthawi zina, iye صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ankagawaniza tsitsi lake lodalitsika m'mbali zinayi, ndipo makutu ake odalitsika ankaonekera pakati pa mbali ziwirizo. Nthawi zina, iye صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ankaika tsitsi lake lodalitsika pamwamba pa makutu ake odalitsika, zomwe zinkapangitsa khosi lake kuonekera komanso kunyezimira.

Tsitsi lake lodalitsika komanso ndevu zake zinali ndi tsitsi loyera lokwana khumi ndi zisanu ndi ziwiri (17) palimodzi. Kusangalala kwake komanso kukwiya kwake kunkaonekera pankhope pake podalitsika, chifukwa khungu lake lolemekezeka linali loyera komanso lowala kwambiri. Chipumi chake chodalitsika chinali chokulirapo (chotakasuka) ndipo ndevu zake zodalitsika zinali zambiri. Iye صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ankasiya ndevu zake kuti zikule ndipo ankameta (kufupikitsa) ndevu zake zapamphuno. *(Ihya Al-Uloom, buku. 2, tsamba. 470)*

Kupambana kwa tsitsi lake lodalitsika

Pambuyo potchula zinthu zopatulika zosiyanasiyana zokhudzana ndi thupi lake lodalitsika, wokonda Mtumiki, A'la Hadrat, A'la Hadrat رَحْمَةُ اللهِ عَلَيْه akunena izi: 'Ndipo cholemekezeka kwambiri mwa izo ndi tsitsi loyeretsa la m'ndevu zodalitsika za Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم. Chikhulupiriro cha Asilamu chikuchitira umboni kuti mitambo isanu ndi iwiri komanso dziko lapansi sizingafike pa ukulu wa tsitsi limodzi limenelo. *(Fatawa Razawiyyah, buku. 21, tsamba. 415)*

Okondedwa abale a Chisilamu! Ngati uwu uli ukulu wa tsitsi limodzi la m'ndevu zake zodalitsika, ndiye kuli bwanji ulemerero wa ndevu zake zodalitsika zonsezo

www.dawateislami.net

Ndipo ngati umu ndi m'mene ziliri ndevu zake zodalitsika, kuli bwanji ulemerero wa Mbuye amene ali ndi ndevu zodalitsika zimenezo.

Kaliyan zulfan wala dukhi dilaa da sahara

Qasam Khuda di meinu sab naalon piyara

Denday nay gawahi zarrey zarrey koh-e-tur day

Vekh de naseebaan waalay jalwey huzoor day

Aaaminah da chan te Haleemah da dulaara

Qasam Khuda di meinu sab naalon pyara

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

Khungu lake lodalitsika

Ee inu omukonda Mtumiki! Pa nkhani ya mtundu wa khungu lodalitsika la Mtumiki Wokondedwa komanso Womaliza wa Allah صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم, zafotokozedwa m'mabuku monga Shumaail Tirmizi, ash-Shifa ndi ena, kuti khungu lake lodalitsika linali loyera kosakanikirana ndi kufiira pang'ono; khungu lake lodalitsika silinali loyera mwathunthu, m'malo mwake, mawonekedwe oyera anali ndi mtundu wofiira pang'ono, ndipo mtundu umenewu umasiliridwa m'dziko lonse lapansi, makamaka ndi ma Arabu. Kunena za ku Paradaiso, mtundu umene umakondedwa kwambiri kumeneko ndi wa golide, ndipo akatswiri achipembedzo olemekezeka akunena kuti: Allah Wamphamvu zonse anampatsa mitundu yonse iwiri imeneyi Mtumiki صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم m'dziko lino, ndipo chifukwa cha kuyera kosakanikirana ndi kofiira pang'ono kumeneku, khungu lake lodalitsika linkawala kwambiri.

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

Mapazi odalitsika a al-Mustafa ﷺ

(Bayan imene inachitika pa 10 Rabi'-ul-Awwal 1442)

www.dawateislami.net

Ee inu omukonda Mtumiki! Sahaba wa Mtumiki, Sayyiduna Abdullah Bin Buraydah رضی اللہ عنہ ananena kuti: Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anali ndi mapazi okongola kwambiri. *(Mawahib al- ladunya, buku. 2, tsamba. 63)*

Dil karo Thanda mera who kaff e paa chand saa

Seeney pe rakh do zaraa tum pe kararon durood

Mawu ovuta: Kaff – pansi pa phazi, Paa – phazi, Chaand saa –ngati mwezi , Zaraa – kwa kanthawi kochepa

Hafiz Ibn Hajar Makki Shaafi'i رَحْمَةُ اللهِ عَلَيْه ananena kuti: Sababah (chala chomwe chili pambali pa chala chachikulu cha kumapazi) chinali chala chachitali kwambiri. *(Madarij al-Nubuwwah, buku. 1, tsamba. 20)* Gawo lakutsogolo lodatsilika la miyendo yake poyandikira kumapazi linali lopyapyala m'njira yoyenera komanso yogwirizana bwino kwambiri.

Kupambana kwa mbali zakutsogolo zodalitsika za miyendo yake

Sayyiduna Suraqah رضی اللہ عنہ ananena kuti: 'Ndinamuyang'anitsitsa Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم pamene iye صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ankasamukira ku mzinda wodalitsika wa Madina; iye صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anali atakwera ngamila ndipo mapazi ake olemekezeka anali m'zitsulo zopondapo. Gawo lakutsogolo lodalitsika la miyendo yake (potengera kuyera komanso kuwala kwake) inkaoneka ngati mulu wa tende amene wangotuluka kumene m'makoko ake. Kutsitsimuka kwa mapazi ake odalitsika kunali koti anthu oyang'ana ankaona ngati kuti madzi angoyenda kumene pa iwo, ndipo misomali yake yodalitsika inalibe mnofu wambiri. Alakatuli ena a Chiarabu odziwa kulankhula bwino anatchula ubwino ndi ukulu wa mapaziwo motere, kwinaku akuwagwiritsa ntchito ngati njira yoyandikirira kwa Allah m'ma Du'a awo:

Tanthauzo la ndakatuloyi ndi motere: Ee Mbuye Wachifundo! Pa chifukwa cha mapazi odalitsika amenewo amene munalola kuti ayende m'malo okwezeka kwambiri, otchedwa Kaba Qawsayn; chifukwa cha ulemu ndi ukulu wa mapazi odalitsika amenewo, amene mwa iwo munapanga mapewa a zolengedwa kukhala

www.dawateislami.net

ngati makwerero a Utumiki; chifukwa cha kuolowa mtima kwanu, apangeni mapazi anga kukhala okhazikika(olimba) pa mlatho wa Sirat ndipo muwapange kukhala chitetezo kuchokera ku Moto, komanso apangeni kukhala chifukwa chokhalira owongoka ndi otetezeka, Pangani zinthu ziwirizi kukhala chuma chamtengo wapatali kwa ine, ndipo aliyense amene wazigwiritsa ntchito zonsezi ngati mkhalapakati, amakhala wotetezeka komanso wosungika ku chilango ndi mantha a ku Gahena.. *(Al wafa Ibn Juzi, buku. 1, tsamba 15)*

Gorey gorey paaon chamkaa do khuda kay waste,

Noor ka tarka ho pyarey, gaur ki shab taar hai

Ndemanga ya ndakatulo ya Raza: A'la Hadrat رَحْمَةُ اللهِ عَلَيْه akupempha pa bwalo la Mtumiki Wokondedwa: Ya Rasoolallah! صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم usiku wanga m'manda ndi wa mdima; chifukwa cha Allah, ndidalitseni ndi kupezeka kwanu m'manda mwanga, chifukwa mukangotero, kudzera m'mapazi anu owala, manda anga adzawalitsidwa ndipo adzadzaza ndi kuwala.

Kupamaban kwa mapazi odalitsika

Sayyiduna Ali رضی اللہ عنہ ananena kuti: Pamene Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم amkayenda, iye amkapanga motero thupi lake lodalitsika litapendekera kutsogolo, Ngati kuti akutsika kuchokera pamalo okwera (monga momwe tsinde la duwa limapindikira), ndipo amakweza mapazi ake odala mwachangu, mwamphamvu, komanso mwamsanga.

Sayyiduna Abu Hurayrah رضی اللہ عنہ anati: Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم nthawi zonse ankaponda ndi phazi lake lonse lodala pansi. Sindinaonepo aliyense woyenda mwachangu m'njira kuposa Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم, zinkaoneka ngati nthaka ikupindika pansi pa mapazi ake odala, ndipo iye صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ndipo iye ankayenda mwachizolowezi popanda vuto lililonse. Ndiponso, akamayenda ndi Masahaba رضی اللہ عنہم, ankawauza kuti aziyenda patsogolo pake ndipo amkati, 'Siyani mpata pa mbuyo panga wa angelo.' *(Madarij al-Nubuwwah, buku. 1, tsamba. 23)*

www.dawateislami.net

Kupambana kwa Na'layn zodalitsika

Sayyiduna Abdullah Bin Abbas رَضِیَ اللّٰہُ عَنۡہُمَا Nsapato zodala za Mtumiki Wokondedwa صَلَّی اللّٰہُ عَلَیۡہِ وَاٰلِہٖ وَسَلَّم zinali ndi zingwe ziwiri zomwe zinali zomangiridwa ndi malamba awiri. *(Ibn Majah, buku. 4, tsamba. 166, Hadith. 3614)*

Mufti Ahmad Yar Khan Na'eemi رَحۡمَۃُ اللّٰہِ عَلَیۡہ analemba mafotokozedwe a Hadith imeneyi kuti: Nsapato iliyonse ya Mtumiki Wokondedwa صَلَّی اللّٰہُ عَلَیۡہِ وَاٰلِہٖ وَسَلَّم inali ndi zingwe ziwiri, ndipo chingwe chilichonse chinali ndi malamba awiri. Chimodzimodzinso, nsapato za Sayyiduna Abu Bakr Siddeeq ndi Sayyiduna Umar رَضِیَ اللّٰہُ عَنۡہُمَا zinali zofanana ndi zimenezi. M'masiku amenewo, mwambo wovala nsapato za sandasi unali wofala, makamaka nsapato za zingwe. Zingwe zonse ziwiri zachikopa za nsapato zodala za Mtumiki Wokondedwa zinkadutsa pakati pa chala chachikulu ndi chala chachiwiri cha kumapazi. Zimkamangiridwa mbali zonse za kumanja ndi kumanzere kwa mbali yakutsogolo ya phazi. *(Miraat-ul-Manajeeh, buku. 6, tsamba. 141 – 144)*

Kya Imamey ki ho biyan a'zmat

Teri nalayn taj-e-sar Aaqa

صَلُّوۡا عَلَی الۡحَبِیۡب صَلَّی اللّٰہُ عَلٰی مُحَمَّد

Kubadwa kwa Mtumiki Wokondedwa ﷺ

(Bayan imene inachitika pa 11 Rabi'-ul-Awwal 1442)

Chifundo chachikulu kwambiri

اَلۡحَمۡدُ لِلّٰہ! Mwezi wonse wa Rabi'-ul-Awwal ndi mwezi wa chifundo ndi madalitso, chifukwa kubadwa kwa Mtumiki womaliza wa Allah صَلَّی اللّٰہُ عَلَیۡہِ وَاٰلِہٖ وَسَلَّم kunachitika m'mwezi umenewu. Mtumiki Wolemekezeka صَلَّی اللّٰہُ عَلَیۡہِ وَاٰلِہٖ وَسَلَّم anabwera padziko lapansi ngati chisomo komanso chifundo cha Allah, ndipo ndithudi, tsiku limene chifundo cha Allah Wamphamvu zonse chatsika ndi tsiku lachisangalalo ndi chimwemwe; Allah Wamphamvu zonse akunena mu Qur'an yopatulika kuti:

www.dawateislami.net

قُلْ بِفَضْلِ اللّٰهِ وَبِرَحْمَتِهٖ فَبِذٰلِكَ فَلْيَفْرَحُوْا ؕ هُوَ خَيْرٌ مِّمَّا يَجْمَعُوْنَ ﴿۵۸﴾

Nena (Iwe Wokondedwa), 'Ndi chifukwa cha chisomo cha Allah komanso chifundo Chake; ndipo pa zimenezi iwo asangalale.' Zimenezi n'zabwino kuposa zonse zimene iwo (asonkhanitsa) chuma.

[Kanz-ul-Iman (kumasulira kwa Quran)] (Gawo 11, Surah Yunus, vesi 58)

Lamulo loti tisangalale pa chisomo komanso chifundo cha Allah Wamphamvu zonse likuperekedwa ndi Qur'an, monga momwe kwanenedwera m'vesi lomwe latchulidwa m'mbuyomu. Ndiye kodi alipo wina aliyense amene ali chifundo chachikulu chochokera kwa Allah Wamphamvu zonse kuposa Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم? Iye صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ndithudi ndiye chifundo chachikulu koposa cha Allah Wamphamvu zonse:

وَمَاۤ اَرْسَلْنٰكَ اِلَّا رَحْمَةً لِّلْعٰلَمِيْنَ ﴿۱۰۷﴾

Ndipo Ife sitinakutumize iwe (E Wokondedwa) koma kuti ukhale chifundo kwa zolengedwa zonse.

[Kanz-ul-Iman (kumasulira kwa Quran)] (Gawo 17, Surah Al-Anbiya, vesi 107)

Sahaab-e-rehmat-e-Baari hay baarween tareekh

Karam ka chashma-e-jaari hai baarween tareekh

(Zauq-e-Na,at, tsamba. 121)

Madalitso pa nthawi ya kubadwa kolemekezeka

Ndiloleni ndikufotokozereni nkhani zina zolimbitsa chikhulupiriro zokhudzana ndi kubadwa kwa Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم. Zatchulidwa m'buku la Mawahib al-Ladunniyyah kuti: Chinthu chimodzi chapadera cha Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ndi chakuti, mabuku opatulika omwe

www.dawateislami.net

anavumbulutsidwa Qur'an yopatulika isanadze, anali ndi uthenga wabwino wa kudza kwake kodala padziko lapansi. *(Mawahib al-Ladunniyyah, buku 2, tsamba. 272)*

Mubarak ho Habeeb-e-Rabb-e-Akbar aane waala hay

Mubarak Anbiya ka aaj afsar aane waala hay

Jo hai sardaar aalam ke sabhi sajda guzaaron ka

Khuda ka aaj woh sacha sanaagar aane waala hai

Ndiyesetsa kufotokoza m'njira yosavuta zimene bambo a Ala Hadrat, Maulana Naqi Ali Khan رَحْمَةُاللهِ عَلَيْه analemba:

Pamene Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم Pamene Mtumiki Wokondedwa (mtendere ndi madalitso a Allah zikhale pa iye) anali m'mimba mwa amayi ake olemekezeka, angelo anamanga ziwanda ndi maunyolo ndipo anaponya mpando wachifumu wa Iblees m'nyanja, kumulanga kwa masiku makumi anayi (40). Pa nthawi ya kubadwa kulemekezeka kwa Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم, kuwala kodabwitsa kunaonekera ndipo kuwala kwake kunapangitsa kuti anthu okhala ku Makkah athe kuona nyumba za ku Syria. Pa nthawi ya kubadwa kwake kulemekezeka, nyenyezi zinayandikira kwambiri pansi moti anthu oyang'ana ankaona ngati nyenyezizo ziwagwera. Atangobadwa kumene, iye صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم, anagwada pansi modzipereka kwa Allah. Pa nthawi ya kubadwa kwake, agogo ake, Sayyiduna Abdul Muttalib رَضِیَ اللّٰہُ عَنْہُ anali ku Ka'bah yodala ndipo anaona Nyumba ya Allah ikugwada pansi molunjika Maqaam a Ibrahim. *(Anwar-e-Jamal-e-Mustafa, tsamba. 181,zosankhidwa)*

Jab ke paida shah-e-ins-o-jaan ho gaya

Door Kaabeh se laus-e-butaan ho gaya

Har sitaara shab-e-mawlid-e-Mustafa

Sham'adaan sham'adaan sham'adaan ho gaya

www.dawateislami.net

Tooti-e-asfahaan, sun kalam-e-raza

Be zaban be zaban be zaban ho gaya

Onetsani chikondi pa Wokondedwayu

Ngati munthu amamukonda wina chifukwa chomuchitira zabwino, ndiye kuti Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ndiye woyenera kwambiri kukondedwa, chifukwa iye صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anatipulumutsa ku Moto ndipo anatitsogolera ku njira ya ku Paradaiso (kutanthauza kuti, anatipulumutsa ku ukafiri ndipo anatipatsa chuma cha Chikhulupiriro). Ndiponso, amene amonetsa chikondi chifukwa cha kukongola, iyenso ayenera kumukonda Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم, chifukwa Allah Wamphamvu zonse anamupatsa kukongola kwa mkati ndi kwa kunja kuposa cholengedwe china chilichonse padziko lonse lapansi. *(Anwar-e-Jamal-e-Mustafa, tsamba. 187,188)*

Inu okonda Mawlid! Kondwererani Mawlid m'nyumba zanu, m'misewu, komanso m'masitolo, muli ndi zolinga zabwino kwinaku mukutsatira malire a Shari'ah, ndipo pezani madalitso ake kwa chaka chonse.

Madalitso a kukondwerera Mawlid

Maulana Naqi Ali Khan رَحْمَةُ اللهِ عَلَيْه anati: Phindu la Mawlid ake ndiloti, nyumba imene Mawlid amawerengedwa amalandira madalitso ndi zabwino, mtendere ndi moyo wabwino, komanso chakudya chambiri kwa chaka chonse. Pa chifukwa chimenechi, anthu a ku Makkah, Madina, Egypt, ndi Yemen nthawi zonse amakhala ndi misonkhano ya Mawlid. Mwezi wodalitsidwa wa Rabi' ul Awwal ukafika, amasangalala, amavala zovala zabwino, amadzikongoletsa ndipo amathira mafuta onunkhira m'zovala zawo. Amachulukitsa kupereka chopereka, amakonza madongosolo oyenera kuti amve nkhani zokhudzana ndi kubadwa kodala kwa Mtumiki, ndipo amaziona zimenezi kukhala chipambano chachikulu komanso ntchito ya mphoto yaikulu. *(Anwar-e-Jamal-e-Mustafa, tsamba. 209 zosinthidwa)*

www.dawateislami.net

N’chifukwa chiyani kubadwa kodalitsika kudachitika Lolemba m’mwezi wa Rabi’ ul Awwal?

Allamah Yusuf Bin Ismail Nabhaani رَحْمَةُ اللهِ عَلَيْه anati: Kubadwa kwa Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم sikunachitike pa tsiku lililonse lodalitsika monga Lachisanu, kapena m’mwezi uliwonse wodalitsika monga Muharram kapena Ramadan, pofuna kuti pasakhale aliyense amene angaganize kuti iye صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anapeza ulemerero chifukwa cha tsiku kapena nthawi imene anabadwayo; m’malo mwake, chowonadi n’chakuti nthawiyo komanso nyengo imeneyo ndi yomwe inapeza ulemerero chifukwa cha Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم. *(Jawahir al-baahar (kumasulira), buku. 3, tsamba. 242)*

Mahboob-e-Rabb-e-Akbar tashreef laa rahay hayn

Aaj anbiya kay sarwar tashreef laa rahay hayn

Kyun hay fazaa muattar! Kyun Roshni hai ghar ghar

Achha! Habeeb-e-Daawar tashreef laa rahay hayn

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

Makhalidwe apadera a Mtumiki Wokondedwa ﷺ

Inu omukonda Mtumiki! Mwa Atumiki Olemekezeka am’mbuyomu, ena anapatsidwa chozizwitsa chimodzi pomwe ena anapatsidwa zozizwitsa zambiri, ndipo Mtumiki wathu Wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anapatsidwa zozizwitsa zambiri koposa onse. Atumiki ena anaonetsa chozizwitsa kudzera m’manja mwawo, ena kudzera mu mpweya wawo, ndipo ena kudzera m’maso mwawo *(Miraat-ul-Manajeeh, buku. 8, tsamba. 162)*, Komabe, udindo wa Mbuye wathu Wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ndi waukulu kwambiri moti (iye mwiniyo ndi chozizwitsa):

Diye mujizey Anbiya ko Khuda nay

Hamara Nabi mujizah ban kay Aaya

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللّٰهُ عَلٰى مُحَمَّد

www.dawateislami.net

Sayyiduna Jibraeel pamaso pa Mtumiki

Zatchulidwa m'buku la Irshad al-Saari, lomwe ndi mafotokozedwe a Sahih al-Bukhari kuti: Sayyiduna Jibraeel عَلَيْهِ السَّلَام anamuyendera Sayyiduna Adam عَلَيْهِ السَّلَام maulendo okwana 12, Sayyiduna Idrees عَلَيْهِ السَّلَام maulendo okwana 4, Sayyiduna Nuh عَلَيْهِ السَّلَام maulendo okwana 50, Sayyiduna Ibrahim عَلَيْهِ السَّلَام maulendo okwana 42, Sayyiduna Musa عَلَيْهِ السَّلَام maulendo okwana 400, Sayyiduna Isa عَلَيْهِ السَّلَام maulendo okwana 10, pomwe anayendera bwalo lolemekezeka la Mtumiki womaliza wa Allah صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم (amene ali Wokondedwa wa Allah) maulendo okwana 24,000. *(Irshad al-Saari, buku. 1, tsamba. 101, Hadith. 2)*

Allamah Muhammad Mahdi Fasi رَحْمَةُ اللهِ عَلَيْه anati: Anamuyendera Sayyiduna Ya'qoob عَلَيْهِ السَّلَام maulendo okwana 4, Sayyiduna Ayyub عَلَيْهِ السَّلَام maulendo okwana 3 komanso Sayyiduna Yusuf عَلَيْهِ السَّلَام maulendo 4. *(Mataala' al-Masaraat, tsamba. 427, zosankhidwa)*

Be liqaa-e-yaar un ko chain aa jaata agar

Baar baar aate nah yun Jibreel sidra chhor kar

Mafotokozedwe a ndakatulo ya Maulana Hasan: Sayyiduna Jibraeel ankakhala wosakhazikika popanda kukumana ndi Wokondedwa wake صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم, ndi chifukwa chake ankakhalira kuyendera bwalo la Mtumiki mosalekeza.

Mtumiki wa dziko lonse

Atumiki ena Olemekezeka عَلَيْهِمُ السَّلَام anatumizidwa ku mitundu ina yake , pomwe Mtumiki wachifundo wa Allah صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anatumizidwa ku chilengedwe chonse; anthu, ma Jinn, ngakhalenso angelo, nyama, ndiponso zinthu zopanda moyo. Monga momwe iye صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ananenera kuti: 'وَاُرْسِلْتُ اِلَى الْخَلْقِ كَآفَّةً' Kutanthauza kuti, 'Ndinatumizidwa ngati Mtumiki ku chilengedwe chonse. *(Muslim, tsamba. 210 – 211, Hadith. 1167)*

www.dawateislami.net

Shaykh Abdul Haq Muhaddis Dihlvi رَحْمَةُ اللهِ عَلَيْه analemba m'buku la Takmil al-Iman kuti: Mbuye wathu Wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anatumizidwa monga Mtumiki kwa ma Jinn onse komanso anthu onse. Pa chifukwa, iye صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم amadziwika kuti ndi (الثقلين) (kutanthauza kuti Mtumiki wa magulu awiriwa (anthu ndi ma Jinn)). *(Takmil Al-Iman, tsamba. 127)*

Mtumiki woyamba ﷺ

Inu okonda Mawlid! Chimodzi mwa zinthu zapadera za Mtumiki wathu Wokondedwa komanso Womaliza صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ndi chakuti pambali pa kukhala mtumiki womaliza, iye ndi woyambanso mwa iwo onse. Izi ndi chifukwa choti iye صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anali woyamba kupatsidwa udindo wa Uneneri. Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anati: 'كُنْتُ نَبِيًّا وَّآدَمُ بَيْنَ الرُّوْحِ وَالْجَسَدِ' Kutanthauza kuti, 'Ndinali kale Mtumiki ngakhale pamene Adam anali pakati pa mzimu ndi thupi. *(al-Jami' al-Sagheer lil-Suyuti, tsamba. 400, Hadith. 6424)*

Farishton ka jhuka sar soo-e-Adam kis ke baa'is se

Tera hi noor tha ae rehnay waalay sabz gumbad kay

Kutsika kwa madalitso

Chinthu chimodzi chapadera cha Mtumiki Wolemekezeka صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم who will intercede for us sinners is that when he صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم amene adzatipemphere chikhululuko ife ochimwa, ndi chakuti pamene anali m'mimba yodalitsika ya amayi ake okondedwa, mvula inagwa mwamphamvu kwambiri moti mitsinje inayamba kuyenda ndipo mitengo inakhala yobiriwira komanso yathanzi, ndipo madalitso anatsika kuchokera mbali zonse pa mtundu wa Quraysh (ngakhale kuti m'mbuyomu panali njala yoopsa). Choncho, chaka chimenecho chinatchedwa 'سَنَةُ الْفَتْحِ وَالْاِبْتِهَاجِ' kutanthauza kuti, chaka chakukulitsidwa kwa zinthu komanso mwayi. *(Anwaar-e-Jamaal-e-Mustafa, tsamba. 172)*

Shaah-e-kawnayn jalwa numaa ho gaya

Rang aalam ka bilkul naya ho gaya

www.dawateislami.net

Muntakhab aap ki zaat-e-waala hui

Naam-e-Pak aap ka Mustafa ho gaya

Dushman-o-dost muflis ghareeb-o-ameer

Tere sadaqey mein sab ka bhalaa ho gaya

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

Lirime lodalitsika la al-Mustafa ﷺ

(Bayan imene inachitika pa 28 Rabi'-ul-Awwal 1442)

Inu omukonda Mtumiki! Pali mwambi wa Chiarabu woti: 'خَيْرُالْكَلَامِ مَاقَلَّ وَدَلَّ' kutanthauza kuti, malankhulidwe abwino kwambiri ndi amene ali achidule koma omveka bwino komanso anthunthu (okwanira). Mtumiki Wokondedwa komanso Womaliza wa Allah صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ndi wapadera ndipo alibe wofanana naye pa makhalidwe ake abwino komanso kupambana kwake. Palibe wina wofanana naye; pambali pa kukhala wolankhula bwino kwambiri kuposa onse, anapatsidwanso chozizwitsa cha 'جَوَامِعُ الْكَلِم' (kufotokoza mfundo zozama komanso zambiri m'mawu ochepa chabe). Allamah Ahmad bin Muhammad Saawi Maliki رَحْمَةُ اللهِ عَلَيْه anati: Allah Wamphamvu zonse anaphunzitsa zinenero zonse kwa Wokondedwa Wake صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم. *(Haashiya-tul-Saawi, buku. 13, Surah Ibrahim, Gawo 13, pansi pa vesi 12, buku. 3, tsamba. 1014)*

Zatchulidwa m'buku la Mirat al-Manajih kuti: Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ali ndi uzindikiri wachibadwa wa zinenero zonse. Pamene Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم amadziŵa malankhulidwe a nyama, miyala ndiponso timiyala, ndiye kodi zingatheke bwanji kuti iye asamvetse malankhulidwe a anthu! *(Mirat-ul-Manajih,buku. 6, tsamba. 335)* Iye ananenanso pamalo ena kuti: Mtumiki wathu Wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم amadziwa zinenero zonse pa nthawi ya moyo wake, ngakhalenso kayankhulidwe ka nkhuni ndi miyala. Nyama zinkapita

www.dawateislami.net

n'kumapereka madandaulo awo kubwalo lake, ndipo ngakhale pakali pano, iye amadziwa zinenero zonse. Munthu aliyense wopereka dandaulo amapereka pempho lake pamanda odala a Mtumiki Olemekezeka m'chinenero chake, ndipo sipafunika wotanthauzira kumeneko. *(Mirat-ul-Manajih, buku. 1, tsamba. 135)*

Woh samajhtey hein boliyaa sab ki, Wohi bhartey hay bholiyaa sab ki

Aao darbar-e-Mustafa ko chalein, khotey sikkey waheen pe chaltey hein

Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ankalankhula mosavutikira ndi anthu ochokera m'madera osiyanasiyana m'zinenero zawo. Malankhulidwe ake odala anali osangalatsa kwambiri, ndipo malinga ndi kaperekedwe ka mawu, iye anali wolankhula mwabwino komanso mozuna kwambiri kuposa onse. Malankhulidwe ake olemekezeka anali odzaza ndi chisangalalo komanso ofewetsa mtima, chifukwa ankakhudza mitima kwambiri ndiponso kuikopa. Pamene iye صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ankalankhula, anali wofunira zabwino kwambiri kuposa onse ndipo nthawi zonse ankadziletsa ku malankhulidwe osayenera.

Sayyiduna Abu Bakr Siddeeq رضی اللہ عنہ ananena modzichepetsa pamaso pa Mtumiki Wokondedwa صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم kuti: Ya Rasoolallah! صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم ndayenda mozungulira Arabia yonse ndipo ndawamva olankhula Chiarabu ambiri momveka bwino pa, koma sindinamvepo wina aliyense wolankhula momveka bwino kuposa inu." Iye صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anati: "Mbuye wanga anandiphunzitsa kulankhula momveka bwino. *(Mawahib al-Ladunniyyah, buku. 2, tsamba. 20)*

Mayn nisaar teray kalam par mili yun to kis ko zaban nahin

Woh sukhan hai jis mayn sukhan na ho, woh bayan hai jis ka bayan nahi

Tere aagey yun hai dabey lachey, fusahaa Arab kay barey barey

Koi jaane munh mein zubaan nahin, nahin, balkeh jism mayn jaan nahin

Ndemanga ya ndakatulo ya Raza: Ya Rasoolallah صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم! Moyo wanga ukhale nsembe pa kalankhulidwe kanu kokongola; palibe amene anapatsidwa lilime lokoma ndi lotonthoza mtima monga lanu. M'malankhulidwe anu mulibe

www.dawateislami.net

kusemphana kulikonse, ndipo nkhani zanu ndi zozama kwambiri moti mawu sangathe kuzifotokoza. E Bwana wanga صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم! pamaso panu, olankhula Chiarabu aluso komanso odziwa kulinganiza mawu ali ngati anthu osalankhula amene alibe malirime; ndipotu, osati lilime lokha, iwo alibenso ngakhale moyo m'matupi mwawo kuti ayime pamaso panu.

Khalifa wachiwiri wa okhulupirira, Sayyiduna Umar Farooq رضی اللّٰہ عنہ analankhula modzichepetsa kuti: Ya Rasoolallah صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم! inu ndinu waluso kwambiri polankhula pakati pathu, ngakhale kuti simunayende kulikonse; kodi chinsinsi cha izi ndi chiyani? Choncho, Mtumiki waluso polankhula صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anati: Chilankhulo cha (Sayyiduna) Ismail عَلَيْهِ السَّلَام chinali chitasiyidwa, choncho (Sayyiduna) Jibraeel anabwera nacho kwa ine, ndipo ndinachiphunzira. *(Al-Wafaa li-ibn Juzi, tsamba. 54)*

Mtumiki wachifundo صَلَّى اللّٰهُ عَلَيْهِ وَاٰلِهٖ وَسَلَّم anati: "Ndinatumizidwa ndi 'جَوَامِعُ الْكَلِم' (mawu ochepa koma otanthauza zambiri). *(Bukhari, buku. 2, tsamba. 303, Hadith. 2977)*

Ee omukonda Mtumiki! ndikufotokozereni mawu amodzi okha kuchokera m'nkhokwe ya 'جَوَامِعُ الْكَلِم' (mawu ochepa koma otanthauza zambiri). Choncho,zanenedwa mu Hadith nambala 10 ya m'buku la Sahih Bukhari kuti: Wokhulupirira weniweni ndi amene okhulupirira ena amakhala otetezeka ku lilime lake komanso ku dzanja lake, ndipo wosamuka ndi amene amasiya zinthu zonse zimene Allah Wamphamvu zonse waletsa.

Wofotokozera buku la Bukhari, Mufti Shareef al-Haq Amjadi رَحْمَةُ اللّٰهِ عَلَيْه Hadith iyi ikuchokera m'ma 'جَوَامِعُ الْكَلِم' amenewo imene Muhaddiseen adaitcha kuti ndi Umm al-Ahadith. Lingalirani! Mawu ake ndi ochepa koma ali ndi matanthauzo ndi nyanja. Gawo loyamba limatitsogolera kupewa kuphwanya ufulu wa anthu komanso kukwaniritsa ufulu wawo wonse, ndipo gawo lachiwiri likunena za kupewa kuperewera kulikonse pakukwaniritsa ufulu wa Allah Wamphamvu zonse. Pambuyo polingalira pang'ono, munthu aliyense wozindikira akhoza kulemba zambiri pofotokoza zimenezi. Ngati Msilamu angagwiritse ntchito magawo awiriwa mu zochita zake, ndiye kuti dera lathu lidzakhala munda wa

www.dawateislami.net

mtendere, ndipo mkati ndi kunja kwa munthuyo kudzawala ngati golide. *(Nuzha-tul-Qaari, buku. 1, tsamba. 309)*

Uss ki piyari fasahat peh behad Durood


Uss ki dilkash balaghat peh lakhon salaam

Uss ki baaton ki lazzat peh lakhon Durood

Uss ke khutbey ki haybat peh lakhon salaam

صَلُّوْا عَلَى الْحَبِيْب صَلَّى اللهُ عَلٰى مُحَمَّد

www.dawateislami.net



Aalami Madani Markaz, Faizan-e-Madinah,
Mahallah Saudagaran Purani Sabzi Mandi, Karachi, Pakistan
UAN +92 21 111 25 26 92 | 0313-1139278 | Ext: 7213
www.maktabatulmadinah.com | feedback@maktabatulmadinah.com